TRUTH CENTERED TRANSFORMATION

MODULE

BUKU LA MPHUNZITSI, PHUNZIRO LA ULALIKI

Truth Centered Transformation-BUKU: LA ULALIKI 4.0 Copyright ©2023 Reconciled World, Phoenix, Arizona, United States of America. www.reconciledworld.org

Ntchitoyi yakhala yotheka pansi pa mgwirizano wa the Creative Commons Attribution–ShareAlike 3.0 license. Muli wololedwa komanso kulimbikitsidwa kugwiritsa ntchito, kukopera, kugawa ndiponso kufalitsa potsatira malamulo ali mmunsimu:

KUTHOKOZA - Muwonetsetse kuti pogwiritsa ntchito kukopera, kugawa ndiponso kufalitsa zolembedwazi musaiwale kulemba kuti: Copyright © 2018 Published by Reconciled World (www.reconciledworld.org) pansi pamfundo za the Creative Commons Attribution–ShareAlike 3.0 license. Ngati mufuna kudziwa zambiri, onani www.creativecommons.org.

Osagulitsa –Osapanga malonda ndi ntchitoyi.

Ngati muli osangalasidwa kuti mumasulire kabuku aka, chonde funsani ku info@tctprogram.org.

Mau onse a Mulungu amene ali mu bukuli atengedwa kuchokera ku buku lopatulika la Mulungu imene inalembedwa ndi, New International Version®, NIV®. Copyright ©1973, 1978, 1984, 2011 by Biblica, Inc.TM.Ikugwirisidwa ndi chilolezo cha Zondervan. All rights reserved worldwide. www.zondervan.com. The “NIV” and “New International Version” are trademarks registered in the United States Patent and Trademark Office by Biblica, Inc.TM.

Musanayambe Kuphunzitsa

Kukonzekela Kuphunzitsa

1. Werengani bwinolomwe **Buku la Mphunzitsi,** mobwerezabwereza ngati ndi kotheka.Ikani chizindikiro kapena lembani pambali mfundo zofunikira kuti zikukumbutseni.
2. Yang'anani **mfundo zikuluzikulu** za phunziro lirilonse kuti mudziwe chomwe ophunzira anu aphunzire mu phunzirolo.
3. Werengani **malemba** onse a mu ndime zonse.
4. Wonesetsani kuti muone kuti ndi **zipangizo** ziti zomwe zifunike mu phunziro lirilonse ndi kuonesetsa kuti mwapanga mabuku a ophunzira komanso kupanga zithunzi zothandizira pophunzitsa zomwe zaonetsedwa mu phunziro.
5. Wonesetsani kuti mukudziwa bwino **ntchito** zonse za mu phunziro (sewero,masewera ndi zithunzi zothandizira pophunzitsa). Mutha kuyesera kuchita ndi apa banja panu ndi anzanu.
6. Tengani nthawi **yopemphera** kuti Mulungu akonzekeretse ophunzira anu, kuti ophunzira amve chimene Mulungu akufuna kuti amve,Komanso kuti Mulungu akuthandizeni kuphunzitsa zinthuzo.Kumbukirani kuti ndi kudzera mwa mphamvu ya Mulungu yokha, mmene tingaone anthu akusinthika.

Mungayigwiritse ntchito bwanji Buku la Mphunzitsi ili

1. **Mfundo Zofunikira ndi Zipangizo:** Phunziro lirilonse yayamba ndi chigawo ichi.
    a. **Mfundo Zofunikira** – Muli mfundo zambiri, zabwino mu phunziro linalirilonse,koma Ophunzira akuyenera kumvetsetsa Mfundo zofukirazi pakutha pa phunziro lirilonse.Ndi kwabwino kudzifunsa nokha ngati mukuganiza kuti ophunzira akhoza kukumbukira mfundo zofunikirazi mukatha kuphunzitsa. Tengani nthawi yobwereza-bwereza mfundo zofunika kuti ziwathandizire kukumbukira.
    b. **Zipangizo** – Zipangizo zoyenera zomwe zigwiritsidwe ntchito zatchulidwa mu phunziro linalirilonse, kuphatikizapo zithunzi ndi zina zowonjezera. Buku la mphunzitsi iyi Iwonetsa nthawi yomwe mukuyenera kuzigwiritsa ntchito. **ZITHUNZI** Ziwonetsedwa motere mu maphunziro.
2. ***Zochita Mphunzitsi:*** *Muli malangizo apadera mu phunziro kuti akuthandizeni potsogolera bwino maphunziro.Izi sizoyenera kugawana ndi ophunzira. Werengani malangizowa musanakaphunzitse kuti mukhale okonzeka kutsogolera zokambirana ndi ntchito. Mafunso ena akhalanso ndi mayankho ake kuti akuthandizireni inu ngati mphunzitsi kuti mudziwe mfundo zoyenera kutsindika ndi ophunzira pophunzitsa.*

Phunziro 1: Kodi Mlaliki ndi ndani?

Mfundo Yotsogolera
Mkhrisitu aliyense ndi Mlaliki. China chilichonse chomwe timapanga kuti wina akhale mkhrisitu ndi ulaliki. Tikuyenera kuitana anthu kuti tigawane nawo za ubale wathu ndi Mulungu.

Zipangizo
- Mkate kapena zakudya zina zomwe zingathe kukonzedwa
- Mabuku a sewero (mabuku atatu)
- Botolo kapena kapu

Chiyambi

ZOKAMBIRANA ZA PA GULU LALIKULU
Zochita Mphunzitsi: *Gwirani mikateina kapena chakudya china. Funsani ophunzira kuti aganizire za chakudya chabwino chimwne adali nacho. Afunseni kuti ndi ndani adawathandiza kupanga chakudyacho. Akayankha mayankho angapo, thandizirani ophunzira kuzindikirano anthu ena ambiri omwe amathandizira kukonza chakudya.*

(Zitsanzo: Wina anasakaniza ufa ndi zipangizo ndi kuphika chakudya. Mlimi anadzala mbewu. Wina anapera mbewu. Wina anakona mphero kuti apere mbewu. Wina anakumbandikupanga nchere.Wina ananyamula nchere ndi mbewu kupita nazo kumalo ogulitsila.Wina anatunga madzi. Wina anatola nkhuni kuti asonkhe moto. Wina anapanga chophikira mkate.)

Zimatenga anthu ambiri kuti chakudya chipangidwe, osati yekhayo amene waphika chakudya.
- Ife timaganiza kuti mlaliki ndi ndani?
- Ganizirani mmene musinthira kukhala mkhrisitu. Anakuthandizani ndi ndanikuti mukhale mkhrisitu. *(Funsani mafunso otsatirawa mwapang'onopang'ono kuti mupereke mpata kwa aliyense kuti alingalire.)*
    - Kodi wina anakupemphelerani inu?
    - Kodi wina anakuthandizani pamene munali ndi chosowa?
    - Kodi anakulalikirani ndani?
    - Kodi munaonapo mkhrisitu akuchita mosiyana ndi anthu ena?
    - Kodi munakula pa banja la chikhrisitu? Kodi anakuphunzitsani inu za Yesu mmene mumakula ndi ndani?
- Anthu onsewa adakuthandizni inu kukhala mkhrisitu. Kodi onsewa anali abusa, atsogoleri a mpingo, kapena amalalikira ngati ntchito yawo?

Inu Ndinu Mlaliki

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKURU
Tiwerenga ndime zitatu za mBaibulo. Ndime zonse zikupereka malangizo wokhudza ulaliki. Tisanawerenge,tiyeni tione kuti malangizo amenewa analembera kwa ndani:

1) Mu ndime,mBuku la Mateyu, Yesu akupereka malangizo kwa ophunzira ake.
    - Kodi Lero, ophunzira a yesu ndi ndani? *(Okhulupilira aliyense)*

2) Mu ndime, mu buku la Akolose,Mtumwi Paulo akulembera kwa anthu Oyera mtima a Mulungu, mu nzinda wa Akolose.
    - Kodi lero, Anthu a Mulungu ndi ati? *(Okhulupilira aliyense ndi mpingo onse)*
3) Mu ndime mu buku la 1Petro, Mtumwi Petro akulembera 'kwa osankhidwa ake a Mulungu [Amene] ali ponseponse.'
    - Kodfi lero, 'Osankhidwa ake a Mulungu' ndi ati? *(okhulupilira aliyense ndi mpingo onse)*
    - Choincho, Ndindandani amene akuyenera kutsatira malangizo onsewa a ulaliki? *(okhulupilira aliyense)*
    - Ndiyeno, Mlaliki ndi ndani? *(okhulupilira aliyense)*

Zochita Mphunzitsi: *Funsani wina awerenge ndime mokweza.Akatha kuwerenga gawo lirilonse la ndime, funsani mafunso otsatirawa.*

- Kodi ndime iyi ikunana chani chani zokhudza mmene tingalalikilire?

Werengani Mateyu 28:18-20

- *Pangani Ophunzira powabatiza ndi kuphunzitsa; chitani izi mu maiko onse.*

Werengani Akolose 4:5-6

- *Khalani a chidziwitso pocheza ndi anthu akunja.*
- *Dziwani mmene mungayankhire.*
- *Gwiritsani ntchito mwayi wina uliwonse mulinawo.*

Werengani 1 Petro 3:15

- *Khalani okonzeka kupereka yankho pa nthawi ina iliyonse, kwa wina aliyense amene angakufunseni zokhudza chiyembekezo chimene mulinacho.*

- Kodi ndime zimenezi zikutiuza chenicheni choyenera kunena kapena kuchita ulaliki? *(Ayi)*

Ndime zimenezi sizikufotokoza zenizeni za mmene tingapangire ulaliki. Zikunena kuti tipange Ophunzira. Zikunena kuti tinene za Yesu kulikonse tingapezeke.Zikunena kuti tikuyenera kukhala okonzeka pamene Mulunghu atipatsampata. Chilichonse tingachite kapena kunena, chomwe chimathandizira kuti anthu akhale a khrisitu ndi ulaliki.

- Mukafotokozera mwan nkhani ya mBaibulo, umenbewo ndi ulaliki.
- Mukakana kuchita chinyengo ku nsika , ndiye wina waona, umenewo ndi Ulaliki.
- Mukanena ndi wina za mmene machimo athu amasokonezera maubale athu, umenewo ndi ulaliki.
- Mukafotokozera mzanu osakhulipilira, kuti mumathandiza mkazi wanu ntchito zapakhomo chifukwa Mulungu akufuna kuti mumukonde, umenewo ndi ulaliki.
- Ngati mungapemphere ndi mnansi wanu, kufunsa Mulungu kuti Amudlitse ndi kumupatsa zosowa zake, umenewo ndi ulaliki.

- Taganiziraninso za anthu amene adakuthandizani kuti mukhale mkhrisitu. Kodi ndani mwa amenewa anali alaliki? *(onse)*

Mkhrisitu aliyense ndi mlaliki. Chilichonse chimene tichita, chomwe chimapangitsa kuti anthu akhale a khrisitu, ndi ulaliki.

Muli ndi Chinachake Choti Mugawane ndi ena

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKURU

Zochita Mphunzitsi: *Funsani anthu atatu kuti awerengesewero. Perekani* ***kapu kapena botolo*** *kwa munthu wathanzi.(mukuyenera kusankha atenga mbali kumayambiliro musanawerenge* ***sewero*** *ndikuwaphunzitsa achite kangapo)*

Chakumwa cha paderadera

MNANSI 1: (*kulira, kuwoneka wodwala kwambiri*) Oo, thupi langa laduwala. Ndakhala otopa kwambiri masiku amenewa.

MNANSI 2: (*kudandaula, kuoneka odwala*). Inde, inenso! Ndimadwala nthawi zonse. Ndikadakonda ndikanapeza mchiritsi kuti ndikadakhala wa thanzi ndi mphamvu!

MNANSI 1: Inenso. Koma ndilibe nthawi yofufudza tsopano. Ndikuyenera ndibwerelenso pa ntchito… ngati ndingathe. (*Ananyamuka mwakachetechete*)

MNANSI 3: *(mwamphamvu anagwira botolo kapena kapu)*. Halo!

MNANSI 2: *(motsitsa)*. Halo. Umadwala dzulo? Ukuoneka wathanzi ndi wa mphamvu tsopano!

MNANSI 3: Ndimadwala, koma ndapeza mankhala ondichiritsa kuti ndisamadwale! chili momu mu chakumwa chapaderadera. Ngati ungamwe ichi, udzakhala wa thanzi ndi wamnphamvu. Kodi ukufuna utakhale nachonso? *(kupereka chakumwa chapaderadera kwa mnansi wachiwiri)*

MNANSI 2: Oo, Inde, Chonde! *(anamwa ndi kukhala wa thanzi ndi mphamvu)* Zikomo kwambiri!

MNANSI 3: Palibe vuto! Ndakondwa kuti ukumva bwino. *(anachoka)*

Tsiku lotsatira, mnansi wachiwiri anakumananso ndi mnansi woyamba.

MNANSI 1: *(mnansi 2 anaona mnansi 1 akuvutika)* Wawo, wasintha! Ukuoneka wathanzi ndi wamphamvu kwambiri!

MNANSI 2: *(akugwirizilabe chakumwa chake)* Inde… Ndachila! Ndichabwino kukhala wa thanzi ndi mphamvu.

MNANSI 1: Ndikukhulupilira kuti ndikhala wa thanzi ndi mphamvu tsiku lina.

MNANSI 2: Ndikukhulupilira chonchonso, nane. Mwina ukhoza kupeza munthu wina amene akhoza kukuthandiza. Chabwino, ndikuyenera kupita. Tsopano kuti ndili ndi mphamvu zochuluka, ndikuyenela kupita kukagwira ntchito. Ndapita! *(mnansi 2 anachoka uku akumwa madzi apaderadera ndi mphamvu zonse. Mnansi 1 amalirabe, akudwalabe.)*

- Kodi munthu wathanziyu anakwanitsa bwanji kuthandiza mzake wodwala? *(anampatsa chakumwa chapaderadera.)*
- Kodi munthu amene akudwala angakhale bwanji wathanzi ndi wa mphamvu? *(ngati wina ampatse chakumwa.)*
- Ndani akadayenera kupereka chakumwa? *(aliyense amene ali ndi chakumwa)*
- Ndani adaonetsa chikondi chochuluka ,Munthu amene apereka, kapena amene sanapereke? *munthu amene apereka)*

Anthu a thanzi anali ndi kanthu kena koti akadatha kugawna ndi munthu odwala. Chimodzimodzinso, tili ndi kanthu kena koti titha kugawana ndi anthu osakhulupilira.

Tili ndi ubale ndi Mulungu. Tili ndi ubale nd Mulungu.Alaliki, thandizani anthu abwere kwa Mulungu.

- Ganizaninso za anthu amene adakuthandizani kuti kuti mufune kutsata Khrisitu.
    - Kodi munthu amene anakupemphelerani ali ndi ubale ndi Mulungu?
    - Kodi munthu amene anakuuzani nkhani ya mBaibulo ali ndi ubale ndi Mulungu?
    - Kodi munthu amene anakufotokozerani za mmene mungatsatire Yesu, ali ndi ubale ndi Mulungu?
- Kudi mukudziona nokha ngati mukuchita zimene anthu awa adachita? Kodi mukudzichita kale?

Mathero

Mkhrisitu aliyense ndi mlaliki. Ife, payekha payekha tili ndi ubale ndi Mulungu. Chilichonse timachita chimene chimathandiza anthu ena kuti adziwe Mulungu, ndi Ulaliki. Mu buku ili tiyankhula zambili za tanthauzo la zimenezi. Tiyankhula za mmene tingalalikilire bwino.

Pamodzi ndi abale, tengani mphindi zochepa kupemphelera anthu amene mukuwadziwa amene sali okhulupilira.

Phunziro2: Cholinga cha Ulaliki

Mfundo Yotsogolera
Cholinga cha Ulaliki ndi kubweretsa anthu mu ubale ndi Mulungu kuti akhale otsatira Yesu.

Zipangizo
- Zinthu zoyenera kuponya-zokwanira kwa wina aliyense kutola chimodzi kapena ziwiri (monga, mapepala okutha, masokosi woyala…)
- Chingwe kapena dengu

Chiyambi

NTCHITO YA GULU LALIKULU
Zochita Mphunzitsi:*Perekani chinachake ka aliyense choti angathe kuponya. Uzani aliyense kuyti aponye zinthu zawo ku cholinga. Adzafunsa kuti cholinga ndi chiyani. Nenani 'Inde! Chimenecho ndiye mfundo ya ntchitoyi! Ndikovuta kufikira Cholinga ngati sukudziwa chimene ukufuna kufikira1! (Nyamulani chingwe kapena dengu. Auzeni ayese kuponyera zinthu zawo kudera pamenepo mongofuna kusangalatsa ndi kumaliza ntchito).*

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
Zochita Mphunzitsi: *Pa zokambirana izi, musadandaule ngati mayankhonkho ndi olondola kapena ayi. Phunziro lonse ifotokozera zimenezi.*
Tisananene za mmene tingalalikilire, tikuyenera kudziwa cholinga cha Ulaliki.
- Kodi alaliki akufuna kuchita chiyani? Kodi Mlaliki angadziwe bwanji kuti achita bwino?
- Imikani manja anu mwamba ngati munanenapo pemphero ya kulapa pamene munakhala mkhrisitu.

Pemphero la munthu ochimwa, ndi kuwulutsa chikhulupiliro chathu mwa Yesu ndi chimene tikukhulupilira mumtima mwathu.Mu pemphero ili:
1. Timavomereza kuti ndife ochimwa ndipo talapa machimo athu.
2. Timapempha chikhulupiliro ndi miyo watsopano mwa Yesu Khrisitu.
3. Timavomereza kukonda Mulungu ndi kumvera Iye nthawi zonse.

- Kodi ndikokwanira kuti wina kungonena pemphero la kulapa?
- Ngati wina anena pemphero la kulapa,koma sanabwerenso ku tchalitchi, kapena kusintha chinachilichonse cha moyo wawo, Tinganene kuti ulaliki unayenda bwino?
- Ngati wina anena pemphero la kulapa koma kukmachimwabe komanso sakufuna kuphuinzira mawu a Mulungu, Kodi iwo anakhaladi akhrisitu?

Tiyeni tione chimene Baibulolinene zokhudza cholinga cha Ulaliki.

Ubale ndi Mulungu

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Werengani Yohane 3:16

- Chifukwa chiyani Mulungu adatuma Yesu ku dziko la pansi?
    - *Chifukwa adakonda dziko lapansi*
    - *Kuti tisatayike koma kukhala nawo moyo wosatha.*

Werengani Yohane 11:25-26

- Kodi Yesu Adanena kuti ndi ndani?
    - Kuuka ndi Moyo
    - Sadzafa (moyo wosatha)

Werengani Yohane 17:2-3

- Molingana ndi ndime yachieiri, Kodi Yesu akutipatsa chiyani?
    - Moyo wosatha
- Ngati Yesu akutipatsa ife moyo wosatha, ndipo Yesu ndi Kuuka ndi Moyo, Kodi tingakhale ndi moyo wosatha popanda kukhala ndi ubale wabwino ndi Yesu?
    - *Ayi*
- Molingana ndi ndime yachitatu, Kodi moyo wosatha ndi chiyani?
    - *Kumudziwa Mulungu ndi Yesu Khrisitu.*

Mulungu Adatumiza Yesu kuti tikakhale kwa muyaya ndi Iye.Mukuyenera kukhala ndi ubale ndi Mulungu kuti mukhale ndi moyo wosatha.

Werengani Aroma 10:9

- Kodi ndi zinthu ziwiri ziti zomwe tingachite kuti tipulumutsidwe?
    - *Kuvomereza ndi pakamwa pako*
    - *Kukhulupilira mumtima mwako kuti Yersu ndi Ambuye*
- Ngati tingonena ndi pakamwa pathu kuti tikukhulupilira, koma osakhulupilira mumtima mwathu,Tapulumutsidwa? *(Ayi)*

Werengani Mateyu 7:21-23

- Kodi munthu anganene kuti Yesu ndi Ambuye wawo koma osadziwa Mulungu? *(Inde)*
- Kodi munthu anganene pemphero la kulapa osamudziwa Mulungu? *(Inde)*
- Kodi angapulumutsidwe? *(Ayi)*

CHIDULE

Kumudziwa Yesu ndi njira yokhayo yopezera Moyo weosatha. Pemphero la kulapa si pemphero lamatsenga imene imatembenuza anthu kukhala a khrisitu.Sumapeza moyo wosatha chifukwa cha kungonena kuti, 'Yesu, chonde khululukirani machimo anga ndi kundipatsa ine moyo wosatha'. Mumaulandira pokhala ndi ubale ndi Mulungu.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALING'ONO

- Kodi mumadziwa bwanji kuti muli ndi ubale ndi wina? (Ganizirani za mkazi wanu, m'bale kapena mlongo, makolo kapena mzanu wapamtima. Siyanitsani chimenechi kwa anthu amene mukuwadziwa – Pulezidenti kapena wina amene mwangokumana naye lero.)

Werengani Yohane 14:21-23

- Kodi tikuyenera kuchita chiyani mkatikati mwa ubale ndi Mulungu? *(Kumvera malamulo a Yesu, mkondeni Iye.)*

- Kodi Mulungu ndi Yesu adzachitanji?
    - *Kubwera kwa*
    - *Kutikonda*
    - *Kukonza nyumba Yake ndi ife tomwe*
- Kodi ubale matyhu ndi Mulungu ufanana bwanji ndi ubale ndi munhtu wina? Kodi zasiyana bwanji?

KUFOTOKOZERA NDI CHIDULE CHAKE

Kukhala ndi ubale ndi Mulungu zimatanthauza kuti timamukhulupilira Iye. Timamukonda Iye. Timamumvera Iye.Timatenga nthawi kunena Naye Cholinga cha ulaliki ndi kubqweretsa anthu mu ubale ndi Mulungu.

Ntchito Yaikulu

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Patangotsala pang'ono kuti Yesu abwelere kupita kumwamba, Anapetreka malangizo kwa Ophunzira Ake kuti apite kukalalikira.

Werenganinso Mateyu 28:16-20 – 'Ntchito Yaikuru'.

- Kodi Yesu adatuma Ophunzira ake kuti achitenji? *(amange otsatira Yesu, Kuwabatiza ndi kuwaphunzitsa.)*

Werengani Yohane 15:8

- Kodi wina angawonetse bwanji kuti ndi Otsatira wa Yesu? *(kubereka zipatso)*

CHIDULE

Tiyeni tiyike maganizo awa pamodzi. Cholinga cha ulaliki ndi kubweretsa anthu mu kuyanjana ndi Mulungu, kuti akhale otsatira wa Yesu. Pamene anthu awonetsa chipatso ,timadziwa kuti ndi wophunzira. Timadziqwa kuti ali ndi ubale ndi Mulungu.

Chipatso Chja Wophunzira

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULIU

Tiyeni tinene za chipatso ichi.

Mzuimayi Wamasiye Amene Adaonetsa Chipatso

Mwamuna wake atamwalira, Nagamani amafuna atafa. A kubanja kwa mwamuna wake anamuthamangitsa.Iye anabwelera kumudzi kwawo ndi ana aang'ono awiri. Ndipo anasauka ndipo analibe chiyembekezo. Wokhulupilira mtchalitchi adauza abusa Paulo zokhudza Nagamani. Abusa Paulo adamuyendera mzimayiyu. Mzimayi adafunsa abusa Paulo,Kodi choyenera kukhalira mmoyo ndi chiyani? Iwo adamuuza, 'Mukuyenera kukhala mmoyo chifukwa cha Mulungu ndi ana anu,osati chifukwa cha inu nokha.'Mpingo unayamba kusamalira Nagamani ngati banja. Analipilira ana awo sukulu. Amapemphera naye pamene ali ndi nkhawa.Anampatsa makina osokera. Ndi makina amenewa, Nagamani amakwanitsa kupeza ndalama Akamasoka zovala. Amapeza ndalama zokwanira kulipilira mwana wake wa mkazi sukulu ndi kuthandiza pakhomo pake. Anaona ,mmene mpingo udamukondera ngakhale sanali mkhrisitu, Chifukwa cha ichi, Nagamani adapereka moyo wake kwa Yesu. Adatulukamo mu nkhawa yake. Adayamba kupita nawo ku mapemphero. Amapereka ndalama za ntchito za chikondi. Tsopano, amaphunzitsa atsikana ochokera mmudzi kusoka kuti angathe kudzithandiza mwa iwo wokha. Amathandiziranso kuphika zakudya za azimayi ena amasiye mu mpingo. Nthawi zina amaperekanso zovala.

- Ndi mtundu wanji wa chipatso umene Nagamani adaonetsa atapereka moyo wake kwa Yesu? (Kodi munganene bwankji kuti anali pa ubale ndi Mulungu?)
    - *Anachoka mu nkhawa(chisangalalo)*
    - *Amapita ku tchalitchi*
    - *Adaonetsa chikondi kwwa ena (kupereka ndalama, chakudya, zovala, kuphunzitsa ena kusoka.)*

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALING'ONO

- Ganizirani za moyo wanu ngatyi mkhrusitu. Fotokozerani mmene moyo wnu wasinthira chifukwa choti munamulandira Yesu. (Mwa chitsanzo, muli ndi khumbo lofuna kuphunzira mawu aMuliungu? Kodi mumadzimvera chisoni mukachimwa?)
- Zipatso zina ndi ziti zimene Ophunzira amakhala nazo?

(Ngati gulu lifuna mfundo,mphunzitsi atha kuwathandizira pogwiritsa ntchito zitsanzo izi)

Akufuna kuphunzira
Amakhumudwa/kulapa akachimwa
Wodzichepetsa ndi umunthu
Kukhululuka akalakwiridwa
Kuyesa kumanganso maubale omwe adavuta
Kuyesetsa kumvera Baibulo
Kuthandiza ena makamaka osauka
Kumanga ubale ndi akhrisitu ena
Kufuna kulemekeza Mulungu mu nyengo zonse
Kuika zosowa za ena choyamba
Kuwerenga Baibulo ndi kupemphera
Kukhulupilira Mulungu pa mavuto
Amgawiritsa ntchito zinthu kulemekeza Mulungu
Kuyesetsa kuti anthu adziwe kuti ndi mkhrisitu
Kupita ku tchalitchi
Kukhala ndi nthawi yokhala ndi Mulungu

KUFGOTOKOZERA NDI CHDULE

Zochita Mphunzitsi: *Ngati nkotheka, Lembani mfundo ya chipatso imene gulu lasankha pa bolodi loyera.*

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

- Ganizirani za chipatso mudachitchula.Kodi chipatso chimenechi chionentseredwe tsopano kapena moyo winawo tikadzafa? *(Panopa)*
- Kodi chipatso ichi chiwonetserdwe Lamulungu lokha, kapena tsiku linalililonse? *(Tsiku linalililonse)*
- Kodi wina ndi mkhrisitu ngati anena pemphero la kulapa koma osabala chipatso china chilichonse? *(Ayi)*

Ophunzira weniweni amabala chipatso. Amakonda Mulungu.Amayesetsa kumumvera ndi kumukondweretsa.

Mathero

Cholinga cha ulaliki ndi kubweretsa anthu mu ubale ndi Mulungu, kuti akhale Ophunzira. Osati ndi kupeza munthu kuti anene pemphero la kulapa. Kuyankhula mawu ena ake sizitanthauza kuti munthu wapulumutsidwa ndipo ali ndi moyo wosatha. Timadziwa anthu kuti ndi Ophunzira akawonetsa chipatso.Izi zimatanthauza kuti moyo wawo wasintha chifukwa akutsatira Yesu. Izi zikachitika, Timadziwa kuti ali ndi ubale ndi Mulungu ndipo ali ndi moyo wosatha.

KUUNIKIRA KWA MJUNTHUN PAYEKHA

- Kodi mukudziwa anyhu amene amanena kuti ndi a khrisitu,koma samaonetsa chipatso? Tengani nthawi pang'ono muwapempherele.
- Nanga inuyo bwanji?Kodi wina athakukuzindikirani inu ngati Ophunzira wa Yesu ndi chipatso chanu?

Phunziro3: Ulaliki Ulingati Ulimi

Mfundo Yotsogolera
Ulaliki ndi ndondomeko ngati Ulimi. Chifukwa anthu ambiri, chisankho cha kutsata Khrisitu sichimachitika akangomva kamodzi.

Zipangizo

- Ndondomeko ya makadi a Ulaliki (makadi 6)Process of Evangelism cards (6 cards)

Chiyambi

Mu phunziro lathali taphunzira kuti cholinga caha Ulaliki ndi kubweretsa anthu mu ubale ndi Mulungu kuti akhale Ophunzira. Tsopano tiyeni tinene za mmene anthu angakhalire Ophunzira.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALING'ONO
Zochita Mphunzitsi: *Pang'ono pang'ono werengani mafunso awa mokweza. Perekani mpata kwa anthu kuti alingalire pamene mukuwawerengera.*

- Kodi ndani anakuuzani za Yesu? Kodi zinachitika liti?Kodi munabwera kwa Yesu mutangomva kamodzi za Iye, kapena munamva mobwerezabwereza?
- Ndani adapemphera nanu kuti mulandire Yesu?Kodi zidachitika bwanji?
- Ngati mudakula pa banja loopa Mulungu, mungakumbukire nthawi kapena zochitika pamene mudasankha kupanga chikhulupiliro chanu mwa Yesu, chinthu chabwino kwambiri mmoyo wanu? Chidachitika ndi chani?

KUPEREKA LIPOTI
Zochita Mphunzitsi: *Kuti mupereke lipoti, funsani anthu kuti aimike manja awo pamene mukufunsa mafunso awa.*

- Muliopo angati mwa inu amene adakulira m'banja la chikhrisitu?
- Mulipo angati a inu amene adaphunzira za Yesu kuchokera kwa winawake kunja kwa banja lanu?
- Mulipo angati a inu amene munakhgala mkhrisitu mutangomva za Mulungu kamodzi kokha?
- Mulipo angati a inu amene mudadziwapo akhrisitu ena kwa zaka zochuluka, musadapereke moyo wanu kwa Mulungu?
- Mulipo angati a inu mudadutsa mu nyengo zovuta kuti muzindikire kuti mumasowekera Ambuye kuti asinthe moyo wanu?
- Ndi angati a inu mudalibe ndi zambiri zoti muphunzire kuti mungakhale bwanji mkhrisitu mutatha kunena pemphero la kulapa?

CHIDULE
Anthu ambiri samakhala Ophunzira a Yesu Kudzera mu kumva Ulaliki kamodzi. Ichi ndi choona ngakhale kwa iwo adakulam'banja la chikhrisitu. Mulungu amagwiritsa ntchito zinthu zambiri pobweretsa anthu kwa Iye mwini.

Ulaliki Uli ngati Ulimi

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Mu Buku ili tifananitsa Ulaliki ndi dongosolo la ulimi. Yesu adagwiritsa ntchito zitsanzo zambiri kulima kapena ulimi kuti anene zokhudza zinthu za Uzimu. (Mpesa ndi minga – Mateyu 7:16-20; Munda wa mpesa – Yohane 15:1-8; Tiligu ndi Nansongole – Mateyu 13:24-29; kudzala mbewu – Marko 4:1-9 ndi kukolora – Mateyu 9:37, Luka 10:2.)

Werengani Mateyu 9:35-38.

- Kodi Ambuye a zokolora ndi ndani? *(Mulungu)*
- Kodi antchito ndi ndani? *(ndi ife pano)*
- Kodi zokolora ndi chani? *(anthu omudziwa Yesu ndi Ophunzira ambiri)*

Titha kutenga anthu onse osakhulupilira ngati munda wa Mulungu, ndipo ndife atchito ake. **Ulaliki uli ngati Ulimi. Zokolora ndi Ophunzira amene abeleka zipatso**. Mu Buku ili lonse tiphunzira Ulaliki poganizira za Ulimi.

- Mu Ulimi, Kodi antchito achitenji kuti akolore zochuluka? *(kusamala nthaka,kudzala mbewu, kuthilira, kuchotsa tchire,kusamalira mbewu za tsopano, kukolora)*
- Kodi iyi ndi ndondomeko yochedwa kapena yachangu? *(yochedwa)*

NTCHITO YA GULU LALIKULU

Zochita Mphunzitsi: *Yalani 'Makadi a ndondomeko ya Ulaliki' pansi. Sankhani ena aziike moyenera. Tsopano werengani mutu mmagawo onse(osindikizidwa) ndi kufotokozera mwachidule matanthauzo ake.*



Kusamala nthaka
Kufewetsa mitima kwa Mulungu



Kudzala mbewu
Kulalikira uthenga



Kudikilira mbewu
Kudikilira pamene, Mulungu akugwira ntchito



Mbewu yatsopano
Kuyitana anthu atsate Yesu; Ngati asankha kutsatira, ndiye kuti ndi mbewu zatsopano

Kuthilira mbewu zatsopano
Kuthandiza okhulupilira atsopano kukula

Chipatso
Ophunzira akuwonetsa chipatso

Ulaliki suli mu ndondomeko yomveka bwino nthawi zonse. Mwa chitsanzo, anthu atha kumva za Yesu, koma mitima yawo itha kukhalabe yowuma. Ndondomeko izi ndi njira zothandizira kuti tiganize mmene tingalalikilire.

ZOKAMIRANA ZA GULU LALIKULU

Tiyeni tigwiritse ntchito mfundo izi ku nkhani yowona ya ulaliki. Pamene mukumvetsera, yeserani kulingalira mbali za nkhani mmene zikugwirizirana mmagawo onse.

Ling

Ling adakula pa banja la chipembedzo cha Chibuda. Pamene adapita ku sukulu ya ukachenjede,amavutika kupeza ndalama zolipilira sukulu. Banja lake sidali yachuma. Amadandaula kwambiri zokhudza ndalama ndgati angathe kupitiliza sukulu yake moti samagona usiku.Adayesa njira zonse kuti apeze tulokoma sizimatheka konse. Tsiku lina, adakumana ndi gulu la a khrisitu mu bwalo. Amasewera mpira wa miyendo. Adamuyitana kuti asewere nawo ndi kupita pamodzi naye kukamwa khofi. Kenako adagawana naye Ling uthenga ndi kumupatsa Baibulo. Ling sanasangalatsidwe kuti akhale mkhrisitu. Koma usiku wina atasowa tulo ndi kudandaula, anaganiza zoyesera kuwerenga Baibulo.Atamaliza kuwerenga Baibulo kwa kanthawi, anamva mtendere. Adakwanitsa kugona usiku onse wosalawo. Iye adapitiliza kuwerenga Baibulo kuti azigona mwa mtendere usiku uliwonse. Amzake wosewera mpira aja adachoka mu mzinda muja, koma adamudziwitsa Ling ku guliu lina la a khrisitu. Akhrisitu awa adakhalanso amzake. Iwo adayankha mafunso ake okhudza Mulungu. Patatha miyezi yambiri, ndi kuwerenga ma uthenga anayi,Ling adalandira Khrisitu ngati mpulumutsi wake. Amzake atsopano adamuwonetsera Ling mmene angapemphelere, kukhulupilira, ndi kutsata Yesu mmadela onse a moyo. Ling adauza banja lake zokhudza Yesu.Banja lake sinali yokondwa ndi ganizo limeneri, koma anamulola kuti apitilize ngati Mkhrisitu – koyamba. Kenako mayi ake a Ling anamwalira, ndipo banja lake limayembekezera Iye kuti awalambire pa mwambo wawo wa maliro. Ichi ndi chikhulupiliro cha Chibuda. Ling amadziwa kuti akuyenera kupembedza Mulungu Yekha, ndiye choncho adakana kupembedza pa guwa la mayi ake. Chifukwa cha ichi, bambo ake ndi abale ake adamuka kuti salinso m'banja limodzi. Ngakhale izi zidamukhumudwitsa Ling kwambiri, andapitilizabe kutsata Yesu mokhulupilika. Iye adapitiliza kuwonetsera chikondi ku banja lake. Patapita zaka, ataona kudzipereka kwa Ling polemekeza ndi kusamalira bambo awo, banja lake lidamulandiranso kachikena. Ubale unayambanso kuchira, koma banja Ling sikufunabe kutsata Yesu. Ling amawa pemphelerabe.

- Kodi a khrisitu adasamala bwanji nthaka? Kodi adachita chiyani asadamuuze Ling za Yesu? (*adasewera mpira wa miyendo, amacheza naye*)
- Kodi ndi mbali iti ya nkhani imakhudza kudzala mbewu? *(pamene analalikira uthenga ndi kupereka Baibulo.)*
- Kodi zinatenga nthawi yayitali bwanji kuti Ling akhale Mkhrisitu? *(miyezi yambiri)*
- Kodi Mulungu amatani pamene Akhrisitu amadikilira mbewu kuti imere? Kodi ndi mavuto ati amene adampangitsa Ling kuwerenga Baibulo? *(samagona, kudandaula za ndalama.)*
- Kodi ndi mbali iti ya nkhani imakhudza mbewu yatsopano? *(pamene Ling adalandila Yesu)*
- Kodi adathilira mbewu yatsopano ndi ndani? *(gulu lachiwiri la akhrisitu)* Kodi adachita chiyani kuti athilire mbewu yatsopano? *(Adamuwonetsera mmene angatsatire Yesu mmadera onse a moyo)*
- Kodi ndi chipatso chiti chomwe Ling adasonyeza?
    - *Kuwerenga Baibulo/ adaphunzitsidwa*
    - *Adagawana Uthenga ndi a pa banja pake*
    - *Kunana kupembedza aliyense koma Mulungu yekha*
    - *Kusonyeza chikondi atakanidwa*
    - *Kulemekeza ndi kusamalira anthu ake.*

Ling adaphunzira kusankha ndi kukhulupilira akhrisitu ena. Mulungu adfagwiritsa ntchito anthu awa kudzala mbewu ya Uthenga. Mulungu adagwiritrsa ntchito mavuto a Ling kuti athandizire Ling kudziwa kuti akusowekera

mpulumutsi.Mu nthawi yake, Ling adapereka moyo wake kwa Yesu. A khrisitu ena adathandizira Iye kuti akulebe Ndicholinga choti abale zipatsoza Chiyero ndi chikondi.

KUUNIKIRA KWA MUNTHU PAYEKHA

- Ganizirani za munthu mmodzi kapena awiri mmoyo mwanu amene sanadziwebe Yesu.
- Kodi munthu aliyense Ali mlingo uti? (Ali ndi mitima yowuma? Kodi ali ndi chidwi ndi zinthu za uzimu? Kodi akumva kusowekera kwa Mpulumutsi? Kodi adamvapo kuti Yesu ndi Ndani? Kodi akudziwa kuti kukhala mkhrisitu ndi chani?)
- Mufunse Mulungu kuti muchite chiyani kuti mukasamale nthaka ndi kudzala mbewu.

KUPELEKA LIPOTI

Zochita Mphunzitsi: *Itanani anthu kuti afotokozere ngati angakonde.*

Mulungu Amapangitsa Zinthu Kukula

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Yang'ananinsopa Mateyu 28:19-20.

- Kodi Yesu ananena chani kumapeto kwa kupereka ntchito Yaikulu? *(Ndili ndi Inu nthawi zonse)*
- Kodi Ife tikuchita tokha ntchito ya Ulaliki? *(Ayi. Yesu Alinafe.)*

Yesu analonjeza kukhala ndi ife. Mulungu mwini akugwira nafe ntchiti limodzi ngakhale sitili kumuona Iye.
Werengani 1 Akorinto 3:6

- Mukadyala mbewu, Mungakakamize mbewu kuti zimere? *(Ayi)*
- Amapangitsa kuti mbewu zimere ndi ndani? *(Mulungu)*

Ntchito yathu ngati alaliki ndi kukhala ,'Ogwira ntchito mmunda'. Koma sitingapange kuti zinthu zikule. Mulungu ndi amene amapangitsa kuti moyo watsopano ukule. Iyi ndi nkhani yabwino. Sitikuyenera kudera nkhawa pa kuchita zonse molondola.

Mathero

Ulaliki sumayamba ndikumuuza wina za Yesu. Sizimathera pamene wina wanena pemphero la kulapa. Ndizopitilira pamenepo.Ulaliki ndi ndondomeko yonse yobweretsa anthu mu ubale ndi Mulungu kuti akhale Ophunzira. Ngati Ulimi, ndi ndondomeko ya pang;onopang'ono. Mulungu amatigewiritsa ife ntchito kuti tisamale nthaka ya mitima ya anthu. Amatigwirtitsa ntchito kudzala mbewu ya Uthenga. Amatigwiritsa ntchitoyothilira mbewu zomera kumene pamene zikukula ndi kubala zipatso.

- Kukhala ndi nthawi yothokoza Mulungu chifukwa cha anthu ndi zowawa munakumana nazo mmoyo wanu zimene zinathandizira kuti mubwere kwa Iye.

Phunziro 4: Umoyo Wako Munthu Umathandiza Kusamala Nthaka

Mfundo Yotsogolera

Mmene mungakhalira ngati mkhrisitu,zikhoza kupangitsa kuti anthu acvhite chidwi ndi Uthenga. Mbali ina ,zitha kuwawonetsa chithunzithunzi cholakwika cha Mulungu Mkhrisitu.Tikuyenera kumanga ubale ndi anthu amene si akhrisitu kuti iwo awone kusiyana pakati pa moyo wathu.

Zipangizo

- Kadi ya ndondomeko ya Ulaliki: Kukonzekeretsa nthaka.

Chiyambi

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

- Kodi Mlimi wabwino angawaze mbewu pa malo poti sipadakonzedwe? Chifukwa chiyani kapena chifulkwa chiyani ayi?
- Kodi chinthu choyambilira kuchita mlimiyu ndi chiyani?
- Kodi pali chinthu china chimene akuyenera kuchita asadadzale mbewu?
- Kodi ngati mbewu zadzalidwa pa nthaka yosakhala bwino, chimachitika ndi chani?

Zochita Mphunzitsi: *Wonetsani kadi ya ndondomeko ya ulaliki: kukonzekeretsa nthaka.*

- Kukonzekeretsa nthaka pofuna kudzala mbewu zili ngati kukonzekeretsa mitima ya anthu kuti amve Uthenga.

Monga ngati mlimi amakonzekeretsa nthaka asadadzale mbewu,Mulungu amatigwiritsa ntchito kuti tikonzekeretse mitima ya anthu kuti amve Uthenga. Amachita izi mu njira zitatu: (1) Moyo wathu wa tsiku-ndi-tsiku, (2) Umboni wathu, ndi (3) Pemphero. Lero tiona choyamirila--Moyo wathu wa tsiku-ndi -tsiku.

Moyo Wathu wa Tsiku-ndi-tsiku Umasintha

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Tchalitchi chitangoyambidwa, anthu osakhulupilira adazindikira kuti anthu Mtchalitchi anali osiyana. Buku la Mchitidwe A Atumwi limanena za moyo mu mpingo woyamba.

Werengani Machitidwe a Atumwi 2:42-47.

- Kodi akhrisitu amenewa amachita chiyani chosiyana ndi anthu ena amene awazungulira? *(zodabwitsa ndizizindikiro, amagawira chilichonse, kupereka kwa osowa, adalki osangalala)*
- Kodi zinthu izi zinali zochitika pa mapemphero a Lamulungu zokha kapena zinalinso zinthu zochitika m'moyo wa tsiku-ndi-tsiku? *(moyo wa tsiku-ndi-tsiku)*
- Kodi anthu owazungulira amamva bwani ndi akhrisitu? *(adali 'wodzadzidwa ndi mantha', kuwaona ali wokonderedwa)*
- Kodi chotsatira cha mmene Akhrisitu amakhalira chinali chotani? *(Anthu ambiri adapulumutsidwa)*

Taphunzira kale kufunika kwake kwa kuchita ntchito za chikondi kuti tiwonetsere Chikondi cha Mulungu ku Dera lathu. Mmene timachitira mu ntchito zathu za tsiku ndi-tsiku ndizofunikanso kwambiri.

Zochita za Mateyu zawauza anthu za Yesu

Mateyu amagwira ntchito pa Sukulu ya sekondale. Ophunzira ambiri ndi aphunzitsi anali Asilamu ndi a chi Hindu. Molingana ndi lamulo la m'dziko lawo,Mateyu samaloledwa kuyankhula chikhulupiliro chake cha Chi Khrisitu pa Ntchito. Mateyu adamvera lamulo ndipo sadauze aliyense za Yesu. Komabe, Iye amachitira wina aliyense bwino. Adali owona mtima ndi olimbikira. Iye adali ndi chisangalalo, ngakhale mu nyengo zovuta. Amayesetsa kumwetulira ndi kulimbikitsa ena. Amzake ogwira nawo ntchito adayamba kubwera kwa Mateyu akakhala ndi mavuto. Iwo amadziwa kuti akawamvetsera iwo mwa chikondi ndi kuwapatsa malangizo a mzeru. Tsiku lina,Ophunzira wa Chisilamu adabwera kwa Mateyu ndi kunena kuti, 'Ndikudziwa kuti ndiwe Mkhrisitu,chifukwa ndikuwonakuti ndiwe osiyana'.

- Kodi mukuganiza kuti Ophunzira adadziwa bwanji kuti Mateyu adali Mkhrisitu?

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALING'ONO

Zochita Mphunzitsi: *Funsani funso ndikutchula malo. Gwiritsani ntchito mfundo zina zomwe zalembedwa mu italic nga anthu akuvutika kupeza mfundo.*

- Kodi Mkhrisitu achite bwanji m'malo otsatirawa?
    - Ku Ntchito *(Kodi Mateyu amachita chiyani chomwe chimafanana ndi Yesu? Kodi ndi njira zina ziti zimene wogwira ntchito akadachita ngati Yesu?)*
    - Ku Nyumba *(Kumbukirani zomwe tidaphunzira za cholinga cha Mulungu pa Ukwati ndi Banja.)*
    - Pa Sukulu *(Kodi mungawonetse bwanji chikondi kwa anzanu ophunzira nawo pamodzi? Mphunzitsi wanu? Ana aang'ono?)*
    - Ku Nsika *(Kodi Yesu akadawadulitsira anthu? Kuwalipira mochepa? Kuba?)*
    - Ku Munda *(Kodi tinauzidwa kuti tisamalire motani chilengedwe cha Mulungu? Kuthandiza Ena? Kodi chidwi chathu chikhale chotani pa kulimbika ntchito?)*

LIPOTI NDI CHIDULE

Akhrisitu akuyenera kukhala moyo moyo wosiyana ndi anthu ena.Tikuyenera kukhala ofunitsa koposa ndi kukonda kwa anthu ena. Tikuyenera kukhala ndi umunthu ndi kudzichepetsa. Ngati tingatero, ndiye kuti anthu ena akopeka kwa Khristu ndi kufuna kudziwa zambiri za Iye.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Umboni wa Elam

Pamene ndinali mnyamata ku Congo,ndimamva Uthenga nthawi zambiri. Nthawi zina Umachokera kwa anthu amene amayenda munsewu kapena anthu amene amalalikikira m'basi imene ndimakwera. Ndimadziwa kuti ndinali ochimwa koma ndikaganiza zinthu zina zimenendimachita, ndimanena kwa ine ndekha,'Ayi, kukhala mkhrisitu sibwino sikoyenera kusiya zinthu zimenezi'. Pamene ndinali ku sukulu ya sekondale, ndinakumana ndi nyamata amene adali wosiyana ndi anthu ena. Mmene amakhalira, anali a chikoka kwambiri kwa ine motero ndimafuna nditakhala mzake. Ndidafufudza ndipo adali Mkhrisitu. Ndinali ndi chidwi kwambiri ndi makhalidwe ake moti ndimafuna nditakhala ngati Iye. Sindimafuna kusiya zikhumbu za uchimo, koma mmene mzanga amawonetsera khalidwe lake ndi kuyankhula kwake pa sukulu zinali zopereka chikoka kwambiri kwa ineMoti ndidaganizo zomufuna Yesu kuti Akhale Mbuye wanga.

- Kodi chifukwa chiyani Elam amafuna kukhala mkhrisitu? *(Amafuna atakhala ngati mzake ndipo mzake adali mkhrisitu)*
- Ngati sitikuyesa kumvera Mulungu mu mbali zonse za moyo wathu, Kodi anthu angakopeke kupita kwa Khrisitu? *(Ayi)*

Monga ngati Elkam, anthu ena akopeka kwa Khrisitu pamene awona umboni wa ntchito Yake mu moyo wathu. Komama ngati wina akulalikila za Yesu, koma aliyense akudziwa kuti ndi munthu wankhanza kwa ana awo, kapena amanamiza anthu ku nsika,anthu adzanena kuti, 'chipembedzo chawo sichikuwonetsa kusintha. Akhrisitu ali ngati wina aliyense.' Mmene timakhalira tsiku ndi tsiku, ndi mbali yofunika kwambiri ya umboni wathu. Ndi mbali ya ndondomeko ya ulaliki.

Kumanga Ubale ndi Anthu Omwe sali Akhrisitu

Zochita Mphunzitsi: *Werengani nkhani zotsatirazi.*

Kuthandiza Hule

Mu dera lina munali mtsikana yemwe adali wamasiye. Iye adalibe ndalama, adalibe luso, komanso adalibe makolo woti angamutsogolere. Mtsikanayu adayamba moyo oyenda yenda kuti apeze zosowa za moyo. Ali ndi zaka 22, mtsikanayu adali ndi pakati. Ngakhale akhala akukhala moyo wake wonse kumudzi umenewu, koma anthu amudelali adamukana. Adalibe banja lomuthangatira pa nthawi ya kubereka. Padalibe wina aliyense yemwe angamuthadizire mwana komanso womulangiza kuti achite motani. Koma azimayi a ku tchalitchi ndi amene adamusamalira ku chipatala pamene amathandizidwa. Pamene adabweretsa mwana kunyumba, Adawonesetsa kuti mtsikanayu wamwa tiyi komanso wadya chakudya. Adamuthandiza kuchapa zovala ndi kusamala mnyumba. Anansi anali a mantha. Anati kwa wina ndi mzake,'Mtsikana ameneyu ndi oyenda yenda! Nanga chifukwa chiyani azimayi a tchalitchi akuchita zonsezi? Nanga yankhula naye bwanji?' Koma azimayi a tchalitchi adafotokoza,'Iye adapangidwa mu chifanizo cha Mulungu. Iye ndiwofunika kwambiri kwa Mulungu.' Kenako anthu a mmudzi adati,'Mpingo ukumuwona Iye mosiyana kwambiri ndi ife. Tidamunyazitsa ndi kuganiza kuti ''Mulungu sakumudziwa chifukwa ndi oyenda yenda, koma mpingo wamuwonetsera chikondi''. Ndipo adalemekeza Mulungu. Nayenso mtsikana adali wodzichepetsa chifukwa cha chikondi cha mpingo, koma samakhulupilira kuti adali wofunika pamaso pa Mulungu. Atakumana ndi Abusa, adati,' Abusa, ndikudziwa kuti ndine wochimwa,koma mwana wana ndi olungama. Chonde pemherelani mwana wanga'. Abusa adapemphera ndi kupereka dzina la mwanayo,'Mulungu adalowelerapo'.

Mzimayi wa Chikhrisitu Akumana ndi Anansi ake

Mu dera lina munali asilamu ndi akhrisitu. Magulu awa osiyana samayankhulana wina ndi mzake. Tsiku lina lotentha kwambiri, mzimayi wa chikhrisitu adawona mnansi wake wa chisilamu ali pa dzuwa ndi mwana wake. Mzimayiyu adayima ndi kuyankhula ndi banja la chisilamuyi. Ndipamene adadziwa kuti adatsekeredwa kunja kwa nyumba yawo. Adayitana banjali kuti abwere kunyumba kwawo kuti akazizidwe, koma adakana. Choncho, adapita kunyumba kukatenga madzi ozizira ndi kubwela nawo. Apanso adawayitanira ku nyumba kwawo. Kumapeto kwake banjali lidabwera ndi kukhala mpaka mzimayi wa chisilamuyu mamuna wake adabwera ndi kuwatenga kupita nawo kunyumba. Zitatha zimenezi, Azimayi awiriwa amakhalira limodzi pafupipafupi, ndipo mabanja awo amadyera limodzi.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALING'ONO

- Mu nkhani yoyamba,kodi azimayi a mpingo adachita chinthu chabwino kumanga ubale ndi mtsikana oyenda yenda? Chifukwa chiyani kapena chifukwa chiyani,ayi?
- Mu nkhani yachiwiri, kodi mzimayi wa chikhrisitu adachita chinthu chabwino kumanga ubale ndi mzimayi wa chisilamu?Kapena kulora ana ake kusewera ndi ana a chisilamu?
- Kodi nkhawa zimene akhrisitu angakhale nazo ndi zotani pomanga maubale ndi anthu womwe sali a khrisitu?

KUPEREKA LIPOTI

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Werengani ndime zotsatirazi Zokhudza Yesu Akumanga maubale ndi amitundu.

Werengani Yohane 4:4-18

- Kodi ndi anthu angati amene Yesu amawalalikra mu ndimeyi? *(mmodzi)*
- Kodi mzimayi adabwera kufunafuna Yesu? *(Ayi)*
- Kodi adayamba zokambirana ndi ndani? *(Yesu)*
- Kodi ndi chifukwa chiyani mzimayi adadabwa kuti Yesu adayankhula naye? *(chifukwa adali Msamaria komanso mzimayi)*

Werengani Mateyu 11:19

- Kodi Amzake a Yesu adali ndani? *(ochimwa ndi okhometsa msonkho)*
- Kodi adachita nawo chiyani amzakewa? *(Adadya ndi kumwa nawo limodzi)*
- Kodi Iye akadatha kuchita zimenezi atangokhala mkachisi, kuyembekezara kuti anthu amupeze? *(Ayi, Amayenera kupita kwa iwo)*

Yesu adapita kwa ochimwa, kuyankhula nawo, ndi kudya nawo limodzi. Adachita izi posawerengera kuti khalidwe lawo linali lotani. Adamanga ubale ndi Iwo, ngakhale anthu amadabwitsidwa nazo zimenezi.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALING'ONO

- Ganizirani zifukwa zimene a khrisitu amakanira kukhala pa chimzake ndi anthu amene sali akhrisitu. Kodi Yesu akadatani ndi zinthu zimenezo?
- Kodi mpingo wathu utani kuti umange ubale ndi anthu osakhulupilira? Kodi anthu achite chiyani?

KUPEREKA LIPOTI

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

- Sankhani chinthu chinachake chomwe mungachite ngati mpingo kuti mumange ubale ndi anthu osakhulupilira Yesu Mdela lanu.

Mathero

Tikamvera Mulungu m'mbali zonsre za moyo wathu, anthu ena adafuna kumudziwa Yesu. Koma ngati tingamakhale ngati dziko mmene limakhalira, sitingathe kubweretsa anthu kwa Mulungu.Anthu amafuna kuti awone chosintha chimene Khrisitu achita mwa ife asanamve mawu athu okhudza Uthenga Wabwino. Anthu

Osakhulupilira sangawone mmene timakhalira ngati sitiwafikira kuti tiwadziwe. Tikuyenera kumanga nawo ubale ngati mmene Yesu adachitira.

KUDZIWUNIKIRA WEKHA MWINI

- Mofulumira,funsani Mulungu ngati pali chinthu china mukufuna kusintha kuti muthe kumulemekeza Iye m'mbali zonse za moyo anu. Khalani kwa mphindi imodzi kumvetsera Mzimu Oyera.
- Funsani Mulungu ngati pali chinthu china mukuyenera kuchita kuti muyambe kumanga ubale ndi anthu Osakhulupilira. Khalani kwa mphindi imodzi kuti muwone ngati Akupatsani Mfundo.

Phunziro 5: Umboni Wanu Umathandiza Kukonzekeretsa Nthaka

Mfundo Yotsogolera
Ngati mwakonzeka kugawana ndi anzanu, Mulungu akhoza kugwiritsa ntchito umboni wani kukangitsa wina kuti achite chidwi ndi Ulaliki.

Zipangizo

- Makadi a ndondomeko ya ulaliki (Kusamala nthaka) ndi (mbewu yatsopano)
- Chinthu china choti mungaponye ndi kugwira (Mwa chitsanzo,pepela yopindapinda)

Chidziwitso cha mphunzitsi: Khalani okonzeka kugawa umboni wanu.

Chiyambi

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
Tiyeni tibwereze pang'ono.

- Kodi Mlaliki ndi ndani? *(aliyense)*
- Kodi cholinga cha ulaliki ndi chiyani? *(Kubweretsa anthu mu ubale ndi Mulungu kuti akhale Ophunzira)*
- Kodi ulaliki ndi ntchito yochita nthawi imodzi, kapena ndi dongosolo lalitali? *(adi ndondomeko)*

Zochita Mphunzitsi: *Wonetsani kadi ya ndondomeko ya ulaliki: kukonzekeretsa nthaka.*

- Kodi njira yoyamba yomwe taphunzira ndi iti kuti Mulungu akhoza kutigwiritsa ntchito kukonzekeretsa nthaka ya mitima ya anthu? (Moyo wathu wa tsiku ndi tsiku ndi maubale)

Pemene anthu awona kuti akhrisitu ndi wosiyana ndi ena, ena adzakopeka nafe. Iwo adzafuna kuti adziwe chimene chikutisiyanitsa.

- Kodi wina adakufunsani chifukwa chiyani muli wosiyana?
- Kodi mudachimva bwanji atakufunsani?
- Kodi mudayankha banji?

Kukonzeka kupeleka lipoti

NTCHITO YA GULU LALIKULU

Zochita Mphunzitsi: *Itanani dzina la winawake mkalasi. Ponyani chinthu (mwa chitsanzo, pepala yopindapinda) kwa iwi uku mukunena, 'gwirani'!*

- *Akachigwira, nenani,'Oh, mudakonzeka!*
- *Ngati sadachigwire, nenani, 'Oh, simudakonzeke!*

Werengani 1 Petro 3:15.

- Kodi ndime imeneyi ikulamula chiyani? *(Kulemekeza Khrisitu, khala okonzeka kupereka yankho)*

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Ndi Chifukwa Chiyani muli Wosangalala Kwambiri?

Chisangalalo nthawi zambiri amapita koyenda pa sabata ndi nansi wake, Van. Van sadali mkhrisitu. Tsiku lina Chisangalalo amadya chakudya chake cha mmamawa pa nkhokwe ya chakudya pafupi ndi kunyumba kwawo. Van adabwera nakhala pambali pake. Chisangalalo adamulonjera mwa nsangala. Van adati, 'Chisangalalo, Chifukwa chiyani umakhala okondwa nthawi zonse? Chisangalalo adali wodabwitsidwa ndi funsolo. Akhala akumupempherela Van, koma sadaganizepo zoti angadzanene chiyani ngati Vani adzamufunse za chimene chidampangitsa kuti asiyani ndi anthu ena. Adachita chibwibwi, 'Oh, ndimaganizira chifukwa Mulungu amandikonda'. Patapita nthawi tsiku limenelo, Chisangalalo adaganiza zokonzekera yankho yabwino.

Mukhoza kulimbikitsika kuti Mulungu akupatsani inu mwayi kuti munene umboni ngati muli wokonzeka kutero.Kodi simudamvepo wina akunena akunena, 'Kodi chifukwa cha chiyembekezo mulinacho ndi chiyani?' Koma atha kunena:

- 'Chifukwa chiyani muli wokondwa nthawi zonse?'
- 'Chifukwa chiyaniya simukupita kwa a sing'anga? Kodi sumaopa mizimu?
- 'Kodi mudachita bwanji kuti ana anu akhale olemekezeka?'
- 'Ndtha kukuuza kuti ndiwe mkhrisitu. Kodi chimakupangitsani kusiyana ndi ena ndi chiyani?

Cholinga chanu chanu cha Chiyembekezo

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Pamene wina akuwonetsa kuchita chidwi ndi kuti chifukwa chiyani muli wosiyana, imeneyo ndi nthawi yofunikira kunena umboni wanu. Umboni wanu ndi nkjhani yanu yokhudza Yesu pokupatsani moyo watsopano.Mukufotokoza chifukwa chiyani muli wosiyana kulekana ndikuti mukadakhala wopanda Yesu. Mvetserani nkhani iyi kuchokera pa Yohane mutu 9.

Werengani Yohane 9:6-12

- Kodi munthu wosaona adali wokonzeka kufotokozera zimene Yesu adamuchitira kwa aliyense adafunsa? *(Eya)*
- Kodi munthu wosaona adanena kuti Yesu amuchitira chiyani? *(Ndinali wosaona ,tsopano ndili kuona)*

'Ndidali wakhungu,tsopano ndili kuona', ndi Umboni wake wa munthu wosaona.

Werengani Machitidwe 26:9-16

- Kodi Paulo amakonda chiyani asadakumane ndi Yesu? *(kuzunza akhrisitu)*
- Kodi Paulo adakhala bwanji wosiyana Yesu atamusintha? *(kuwuza anthu za Yesu)*

'Ndimazunza akhrisitu, koma Yesu adandisankha ine ngati mtumiki ndi mboni' ndi umboni wa Paulo.

Werengani Machitidwe 3:6-10

- Kodi umboni wa munthu amene adachilitsidwa ungakhale wotani? *(Ndidali wopunduka,tsopano ndikutha kuyenda.)*

Tiyeni tiwerengenso nkhani ya Ling.

Ling

Ling adakula pa banja la chipembedzo cha Chibuda. Pamene adapita ku sukulu ya ukachenjede,amavutika kupeza ndalama zolipilira sukulu. Banja lake sidali yachuma. Amadandaula kwambiri zokhudza ndalama ndgati angathe kupitiliza sukulu yake moti samagona usiku.Adayesa njira zonse kuti apeze tulokoma sizimatheka konse. Tsiku lina, adakumana ndi gulu la a khrisitu mu bwalo. Amasewera mpira wa miyendo. Adamuyitana kuti asewere nawo ndi kupita pamodzi naye kukamwa khofi. Kenako adagawana naye Ling uthenga ndi kumupatsa Baibulo. Ling sanasangalatsidwe kuti akhale mkhrisitu. Koma usiku wina atasowa tulo ndi kudandaula, anaganiza zoyesera kuwerenga Baibulo.Atamaliza kuwerenga Baibulo kwa kanthawi, anamva mtendere. Adakwanitsa kugona usiku onse wosalawo. Iye adapitiliza kuwerenga Baibulo kuti azigona mwa mtendere usiku uliwonse. Amzake wosewera mpira aja adachoka mu mzinda muja, koma adamudziwitsa Ling ku guliu lina la a khrisitu. Akhrisitu awa adakhalanso amzake. Iwo adayankha mafunso ake okhudza Mulungu. Patatha miyezi yambiri, ndi kuwerenga ma uthenga anayi,Ling adalandira Khrisitu ngati mpulumutsi wake. Amzake atsopano adamuwonetsera Ling mmene angapemphelere, kukhulupilira, ndi kutsata Yesu mmadela onse a moyo. Ling adauza banja lake zokhudza Yesu.Banja lake sinali yokondwa ndi ganizo limeneri, koma anamulola kuti apitilize ngati Mkhrisitu – koyamba. Kenako mayi ake a Ling anamwalira, ndipo banja lake limayembekezera Iye kuti awalambire pa mwambo wawo wa maliro. Ichi ndi chikhulupiliro cha Chibuda. Ling amadziwa kuti akuyenera kupembedza Mulungu Yekha, ndiye choncho adakana kupembedza pa guwa la mayi ake. Chifukwa cha ichi, bambo ake ndi abale ake adamuka kuti salinso m'banja limodzi. Ngakhale izi zidamukhumudwitsa Ling kwambiri, andapitilizabe kutsata Yesu mokhulupilika. Iye adapitiliza kuwonetsera chikondi ku banja lake. Patapita zaka, ataona kudzipereka kwa Ling polemekeza ndi kusamalira bambo awo, banja lake lidamulandiranso kachikena. Ubale unayambanso kuchira, koma banja Ling sikufunabe kutsata Yesu. Ling amawa pemphelerabe.

- Kodi Ling adakumana ndi vuto lanji? *(Adali ndi nkhawa moti amalephera kugona.)*
- Kodi Yesu adamusintha bwanji? *(Kuwerenga Bible kudamuthandiza iye kugona mwamtendere.)*
- Kodi umboni wake wa Ling udali wanji? *(Ndimadandaula kwambiri,sindimagona,koma Yesu adandipata ufulu.)*

CHIDULE

Mu umboni wathu, timawauza anthu mmene moyo wathu wasinthira chifukwa cha Yesu. Umboni ukhoza kukhala mmene Yesu akusinthirani pamene mudangokhala kumene mkhrisitu,koma ziziyenera kukhala choncho.Mutha kunenanso za njira imene Mulungu akuthandizirani kuti musinthe tsopano.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Umboni wa Chisangalalo

Ndiri wa chichepere, ndidaganiza zotsata Yesu. Kuyambira nthawi imeneyo, Yesu akhala akundithandiza kuti ndikhale munthu wabwino. Mwa chitsanzo, Mudandifunsa chifukwa chiyani ndiri wokondwa kwambiri. Mmene ndinali wang'ono, ndimaganiza kuti ndikachita chirichonse molondola, zikadatsimikizira kuti ndine wofunikira ndi wamtengo wake. Ndimakhumudwa ndikalephera kuchita bwino pa sukulu, ndipo ndimamva bwino ndikapambana. Yesu adandithandiza kuti ndizindikire kuti kuchita bwino ndi kusachita bwino pa sukulu sizimandikweza kapena kunditsitsa mtengo kusina ndi anthu ena. Ine ndine wofunikira kale kwa Iye. Ndi chimene chimandipangitsa kukhala wokondwa. Nditha kugwiritsa ntchito luso langa kuthandiza anthu ena mmalo mogwiritsa ntchito iwo kuti ayese kuwonetsa kuti ndine wabwino bwanji. Ndikhala wokondwa kukuwuzabe za Yesu ngati ukusangalatsidwa nazo.

- Kodi Chisangalalo adakumana ndi vuto lanji? *(amakhumudwa akalephera pa sukulu)*
- Kodi adasintha bwanji chifukwa cha Yesu? *(Adamuthandiza kuti awone kuti ndiwofunika ndi wa mtengo wake kwa Iye. Tsopano ndiwokondwa.)*

Umboni wa Mphunzitsi

Perekani umboni wanu.
Wonesetsani kuti ndi waufupi kuti wophunzira asavutike kuutsatira.
Malizani ndi, 'ngati mukusangalatsidwa, nditha kukuuzani zambiri za Yesu.'

- Kodi ndi vuto lanji limene ndakumana nalo?
- Kodi ndidasintha bwanji chifukwa cha Yesu?

NTCHITO YA PAYEKHA PAYEKHA
Iyi ndi nthawi yanu kuti mukonze umboni wanu. Ukuyenera kufotokoza kuti ndinu wosinthika bwanji chifukwa cha Yesu.Ganizirani za mafunso awa:

- Kodi ndi mantha kapena mavuto ati amene Yesu akuthandizani? (mwa chitsanzo,maubale, mantha, zotchinga)
- Kodi moyo wanu wasintha bwanji chifukwa cha Yesu?

Perekani mphindi khumi za chete kuti anthu akonze umboni.

NTCHITO YA GULU LALING'ONO
Yenderani mmagulu aang'ono a anthu awiri kapena atatu ndikugawana umboni wina ndi mzake. Mukamaliza kupereka umboni wanu, dziperekeni kufotokozera zambiri za Yesu.

KUPEREKA LIPOTI
- Kodi chimamveka bwanji kumva nkhani za anthu?
- Kodi chimamveka bwanji kupereka umboni wanu?Chinali chosavuta kapena chovuta kunena?

Mathero

Zochita Mphunzitsi: *Limbikitsani anthu kuti azipereka umboni wawo kugulu lonse. Lolani kugawanaku mpakana mathero a kalasi. Iyi ndi njira yabwino yophunzilira kupereka umboni.*

Tayitanidwa kuti kupatsa anthu ena Chiyembekezo chimene tirinacho. Mulungu atipatsa mwayi kuti tifotokozere chimene Yesu watichitira. Tikuyenera kukhala wokonzeka kuti titero.

Phunziro 6: Pemphero Limathandiza Kukonzekeretsa Nthaka

Mfundo Yotsogolera
Pemphero ndi mbali yofunika ya ulaliki. Titha kufunsa Mulungu kuti akonzekeretse anthu kulandira uthenga. Titha kupemphera ndi wosakhulupilira zokhudza zosowa zawo. Ndipo titha kupemphera kuti tichite mwayi kuti tiwonetse chikondi cha Mulungu ndi kufalitsa uthenga.

Zipangizo
- Kadi ya ndondomeko ya ulaliki: kukonzekeretsa nthaka

Chiyambi

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
Zochita Mphunzitsi:*Wonetsani kadi ya ndondomeko ya ulaliki:kukonza nthaka.*
- Kodi njira ziwiri zoyambilira ndi ziti zimene Mulungu amatigwiritsa ntchito kuti tikonze nthaka? *(moyo wathu wa tsiku ndi tsiku, umboni wathu)*

Pemphero ndi njira ina yokonzekeretsa nthaka ya mitima ya anthu.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALING'ONO
- Kodi ndi ati wosakhulupilira mwakhala muli kuwapempherela? Kodi mwakhgala muli kuwapempherela kwa nthawi yayitali bwanji?
- Kodi mumakonda kuwapempherela bwanji anthu wosakhulupilirawa? Ndi zinthu zina ziti zomwe mumakonda kuwapempherela anthu wosakhulupilira?

KUPEREKA LIPOTI
Lero tiona njira zitatu zomwe tingawapempherele osakhulupilira.
1) Pempherani kuti Mulungu awakonzekeretse kulandira ulaliki.
2) Kupemphera ndi osakhulupilira.
3) Kupemphelera mwai kuti mugawire chikondi cha Mulungu.

Kupemphera kuti Mulungu Awakonzekeretse Anthu Kulandira Uthenga

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
Kumbukirani kuti sitikulalikira uthenga tokha. Sitingakakamize wina kuti akhale mkhrisitu. Ndi Mulungu yekha amene angawakonzekeretse kulandira uthenga.

Werengani 2 Timoteyo 2:25-26, Yohane 6:44, ndi Machitidwe 16:14
- Kuchokera mu ndime zimenezi,kodi tingawapempherele bwanji anthu amene tikufuna kuwafikira? (kupemphera kuti Mulungu atsegule mitima yawo)

Ron ndi Rita

Mosakhalitsa atatha kukwatirana Ron ndi Rita, Rita adayamba kuopita ku tchalitchi ndi kukhala mkhrisitu wamphamvu. Adagawana chikhulupiliro chake ndi mwamuna wake Ron, koma Ron sadapite ku tcalitchi. Kenako Roni adathetsa ukwati ndi Rita. Iye samayankhula nayenso. Rita adapitilizabe kumupempherera Ron tsiku ndi tsiku. Amamupempha Mulungu kuti amukonzekeretse Ron kuti alandire uthenga wabwino. Mzake wina wochokera ku tchalitchi cha Rita amakonda kumuitanira Ron ku chakudya cha masana. Munthu ameneyi adayankhula naye ndi kupemphera ndi Ron. Patatha zaka zambiri, Ron adakhalanso pa ubwenzi ndi mkhrisitu wina amene adakumana naye pa kalasi ya masewero olimbitsa thupi. Mkhrisitu uyunso adamuuza Ron za Yesu. Pamapeto pake, Ron kutatha zaka khumi atathetsa ukwati wake, Ron adalandila ulaliki. Iye adakhala wosangalala mmalo mokwiya ndi kutswinjika. Adalowa mpingo wakudera kwawo ndi kubwerananso ndi Rita. Adayamba kugawana ndi anthu za chikhulupiliro chake mpakana adamwalira.

- Kodi Mulungu adagwiritsa ntchito anthu bwanji kukonzekeretsa nthaka ya mtima wa Ron? *(Rita kupemphera, kufotokozera, ena kupemphera ndi kukhala abwenzi)*
- Kodi Mulungu adayankha pemphero la Rita? Kodi Iye adagwira ntchito mwa Ron? *(Eya)*
- Kodi chikadachitika ndi chiyani kwa Ron, ngati Rita, mzake wa ku tchalitchi ndi munthu wina wa chikhrisitu sadapitilize kupemphera ndi kuyankhula ndi Ron ndi kukhala pa ubwenzi naye, ngakhale samaonetsa chidwi chovomereza? *(Iye sakadamudziwa Mulungu)*
- Alipo anthu amene mwakhala mulikugawana nawo uthenga ndi kuwapempherela koma sadakhalebe mkhrisitu?

CHIDULE

Pamene tikupempherela wina amene sadziwa Mulungu, tikuyenera kupemphera kuti Mulungu awapange kuti akhale wokonzeka kulandira ulaliki. Tikuyenera kupitiliza kupemphera, wosafoketsedwa. Kumapeto kwa phunziro lalero, tikhala ndi nthawi yopempherela anthu amenewa.

Pempherani ndi Anthu Chifukwa cha Zosowa Zawo

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Njira yabwino yokonzekeretsa nthaka ya mitima ya Anthu ndi kupemphera nawo zokhudza zosowa zawo kapena mavuto awo. Tiyeni tiwerenge nkhani ziwiri.

Mzimai Wamasiye3 Amene Adaonetsa Mbewu

Kumbukirani Nagamani? ’Mpingo unayamba kusamalira Nagamani ngati banja. Analipilira ana awo sukulu. Amapemphera naye pamene ali ndi nkhawa.Anampatsa makina osokera. Ndi makina amenewa, Nagamani amakwanitsa kupeza ndalama Akamasoka zovala. Amapeza ndalama zokwanira kulipilira mwana wake wa mkazi sukulu ndi kuthandiza pakhomo pake. Anaona ,mmene mpingo udamukondera ngakhale sanali mkhrisitu, Chifukwa cha ichi, Nagamani adapereka moyo wake kwa Yesu. Adatulukamo mu nkhawa yake. Adayamba kupita nawo ku mapemphero. Amapereka ndalama za ntchito za chikondi. Tsopano, amaphunzitsa atsikana ochokera mmudzi kusoka kuti angathe kudzithandiza mwa iwo wokha. Amathandiziranso kuphika zakudya za azimayi ena amasiye mu mpingo. Nthawi zina amaperekanso zovala.

Mayankho a Yesu pa Pemphero ya Achinyamata

Ngati ntchito ya utumiki, Anyamata awiri awiri adapita khomo ndi khomo kuyendera anansi. Adali achichepere, ndipo ambiri sadayendepo komanso kupemphera pamodzi ndi anthu amene sali akhrisitu chiyambire. Amasowa poyambira kuti akayankhula bwanji ndi anthu kapena kupemphera nawo. Pa nyumba ina, mwana adauza achinyamatawa kuti bambo ake adali mbiya ng'ambe. Achinyamata adapemphera kuti asiye kumwa ndi kubwerera pa banja. Asadamalize kupemphera, bambo aja adalowa mnyumbva, ndikunena kuti akufuna kulapa ndikupereka moyo wake kwa Yesu.

- Pamene Nagamani adakhumudwa, kodi anthu a mpingo adamupempherera pa mkumano wa mapemphero, kapena adapita kwa iye ndi kupemphera naye? *(adapemphera naye)*
- Kodi achinyamata amamva bwanji za kupemphera ndi anthu? *(kusowa poyambira)*
- Kodi Mulungu adawayankha pemphero lawo? *(Eya)*
- Kodi amayenera kukhala ndi mawu anthetemya? *(Ayi)*

Ndi chilengedwe kusowa poyambira ukazipereka kupemphera ndi wosakhulupilira. Izi ndi zina zofunika kukumbukira.

- Pemphero ndi kuyankhula ndi Mulungu za kusamala kwako kwenikweni pa munthu.
- Fupikitsani mapemphero anu.
- Musadandaule zoti Mulungu ayankha kapena ayi. Khulupilirani kuti Mulungu akumvetsera mapemphero anu.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

- Kodi mudadziperekapo kupemphera ndi wina amene sali mkhrisitu? Kodi adachilandira bwanji?
- Kodi phindu yakupemphera ndi osakhulupilira ndiyotani?
- Kodi chingapangitse kuvuta kudziperekja kupemphera nawo ndi chiyani?

KUPEREKA LIPOTI

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Nansi wa Sarah

Panali mzimai mkatikati mwa anansi a Sara amene mwamuna wake adayisiya banja. Sara adapemphera ndi anansi ake kuti Mulungu achize banj kuti banja lawo lithe kubwelera. Mwamuna wa mayiwa sadabwelere. Mmalo mwake, adayithetseratu banja. Sara ndi mamuna wake adapitilizabe kumuwonetsera chikondi nansi wawo. Sara adathandiza kusamalira ana. Mwamuna wake wa Sara adathandizira kubwezeretsa zinthu pakhomopo ndi katundu. Ngakhale pemphero sidayankhidwe, ngati mmene adayembekezera, nansi wake wa Sara adali nacho chonena cha mmene Sara adamusamalirira.

- Kodi Mulungu adamuyankha Sara mmene amayembekezera?
- Pamene mapemphero ake sadayankhidwe mmene amayembekezera, Kodi Sara ndi mamuna wake adachita chiyani? *(Adapitiriza kuwonetsa chikondi)*

Ngati Mulungu sadayankhe pemphero imene mwapempherera osakhulupilira, musadandaule. Izi ndi zinthu zimene mungachite:

- Auzeni mmene mwakhumudwira kuti adutsa mu zimenezi.
- Fotokozerani mmene Mulungu adakuthandizirani mu nyengo yowawa m'mbuyo.
- Atsimikizireni za chikondi cha Mulungu pa iwo.

- Chitani zomwe mungathe kuti muwathandize (Mulungu akutumani INU ngati Omuyimilira)

CHIDULE

Kupemphera ndi anthu ena kumawapangitsa kuti adziwe kuti mumasamala za iwo. Zimawaonetsera kuti mumakhulupilira Mulungu.Sitikuyemnera kukhala ndi mawu abwino. Titha kukhulupilira kuti Mulungu akugwira ntchito mmoyo wa anthu. Izi ndi zoona ngakhale ngati sadayankhe mapemphero monga timayembekezera. Ndipo ngati Ayankha mapemphero, Awona mphamvu Yake!

Pempherelani Mwayi

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

- Ndani akukumbukira zinthu ziwiri zoyambilira zimene tidanena zokhudza pemphero kwa osakhulupilira? *(kupemphera kuti Mulungu awakonzekeretse kumva uthenga, kupemphera nawo pa zosowa zawo)*

Ichi ndi china comaliza chimene tingapemphelere.

Werengani Machitidwe 4:23-31.

- Kodi okhulupilira amapempherela chiyani? *(Mphamvu ndi zozizwa kuti awonetsere mphamvu ya Mulungu ndi ulemelero)*

Werengani Akolose 4:2-6

- Kodi Paulo adawafunsa akhrisitu a ku Akolose kuti apemphelere chiyani? *(kutsegula makoma,mawu abwino, mwayi)*

Mulungu akhoza kubweretsa mwayi kwa ife kuwonetsera chikondi chake ndi kugawa uthenga. Iye akhoza kutipata mawu oti tinene. Akhoza kutilimbikitsa kuti tiyankhule,ngakhale mu nyengo zovuta. Mvetserani ku nkhani iyi,imene mungathe kukumbukira kuchokera mu maphunziro oyamba.

Kulalikira kwa Mkazi wa Membala wa Gulu la Zigawenga

Mu dela lina, mpingo udaganiza zochita ntchito ya chikondi. Adapemphera zokhudza mmene angachitire ndikumva kuti Mulungu amawauza kuti athandize mkazi wa mtsogoleri wa zigawenga mu derslo. Adali ndi mantha, chifukwa mtsogoleri wa zigawengayu adali ndi mbiri yoti amakwiya kwambiri komanso kumenya anthu pa zifukwa zazing'ono. Komabe, mpingo numayenera kumvera Mulungu. Adadikilira mpaka mkulu wa zigawengayu adapita mtawuni, ndipamene adamuthandiza mkazi wake kukolorambewu ndi kumuthandiza kuzisamala kuti akagulitse. Mmene mtsogoleri wa zigawenga adafika kunyumba, adawona mbewu zonse zakololedwa ndipo adayamba kukalipa, "Wachita zimenezi ndani?" Mkazi wake amaopa kumuuza, kuopa kuti atha kubweretsa vuto, koma kenako adawulula kuti a tchalichi ndi amene amuthandiza. Mtsogoleri wa zigawengayu adawuyamba wa ku tchalitchi ndikukayima pa khomo.Abusa adaitana akulu a mpingo kuti awathandizire kenako Abusa adatsegula chitseko ndipo chigawengacho chidalowa. Mudachitiranji zimenezija? Adafunsa. Adayankha nati,amangofuna kuwonetsera chikondi cha Mulungu.Mamunayi adayamba kulira, uku akunena kuti palibe amene adakondapo moyo wake chiyambire. Adagawana naye za Yesu. Iye adakhala mkhrisitu, kutembenuza moyo wake, ndi kupitanso kukatsogolera mabanja asanu ndi imodzi a zigawenga kwa Khrisitu.

- Kodi okhulupilira adapempherera chiyani? *(NTCHITO yanji ya CHIKONDI yoti achite)*
- Kodi mulungu adawapatsa chilimbikitso? *(Eya)*
- Kodi Mulungu adawapatsa mwayi woti agawire uthenga? *(Eya)*

Tikuyenera kupemphera kuti Mulungu atipatse mwayikuti tiwonetse chikondi chake ndi kugawa uthenga. Iye adzatipatsa mpata pa nthawi yoyenera.
`

Mathero

Zochita Mphunzitsi: *Wonetsani kadi ya ndondomeko ya ulaliki: kukonzekeretsa nthaka.*
Kodi Mulungu amatigwiritsa ntchito bwanji kuti tithandize kukonzekeretsa nthaka ya mitima ya anthu?

- Umoyo wathu
- Umboni wathu
- Mapemphero athu

Kodi ndi njira zitatu ziti zimene taphunzira zopemphelera osakhulupilira?

- *Kupemphera kuti Mulungu awakonzekeretse kuti amve ulaliki*
- *Kupemphera nawo pa zosowa zawo*
- *Kupempherela mwayi kapena mpata wofalitsa uthenga ndi kuwonetsa chikondi cha Mulungu.*

PEMPHERO LA GULU LALING'ONO
Gawani magulu a anthu 2-3, ndikukhala ndi mphindi zochepa kupempherera osakhulupilira womwe mukuwadziwa. Komanso pempheleranì wina ndi mzake, mpata,mzeru komanso kulimba mtima.

Phunziro 7: Mwayi Wodzala Mbewu

Mfundo Yotsogolera
Mulungu angathe kupereka mwayi kuti tifalitse uthenga ngati tachita ntchito za chikondi ndi pamene tikuyankhula ndi anthu.

Zipangizo
- Ndondomeko ya makadi a ulaliki. Kudzala mbewu.
- Sewero - Yesu ndi Mkazi wa ku Samaliya.
- Sewero. NTCHITO YOVUTA (MAKOPE AWIRI)

Chiyambi

Zochita mphunzitsi: *Nyamulani ndondomeko ya makadi a ulaliki. Kudzala mbewu.*
Lero tiyamba ndi kunena za kudzala mbewu za uthenga. Mulungu apereka mwayi kuti tifalitse uthenga. Tikudziwa kuti timakhala ndi mwayi wofalitsa uthenga ngati anthu ali ndi chidwi chofuna kuphunzira zambiri za Yesu.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALING'ONO
- Kodi chidakupangitsani poyambilira kuti muchite chidwi ndi za Yesu ndi chiyani?
- Kodi mukukumbukira zokambirana zinazilizonse mudali nazo zokhudza Yesu musadakhale mkhristu?
- Kodi muli ndi vuto kapena chosowa?

KUPEREKA LIPOTI

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
Kumbukirani nkhani za ulaliki zomwe tamva:
- Ling samagona . Iye adali ndi chidwi ndi Baibulo chifukwa idamupanga iye kumva mtendere mpakana adayamba kugona.
- Nagamani adalibe chifukwa chokhalira mmoyo mamuna wake atamwalira. Adali ndi chidwi chofuna kukhala mkhrisitu chifukwa cha mmene mpingo udamuthandizira ngati wa banja limodzi ndikumuthandizira kufikira zosowa zake.

Phunziro ndiyokhudza kuyang'ana mwayi kapena mpata wofalitsira Uthenga. Izi zimachitika chifukwa titha kulumikizitsa ku zimene anthu amadziwa ndi zosowa zawo.Tiwona makamaka, madera awiri amene Mulungu akhoza kupereka mwayi:
- kudzera mu ntchito za chikondi
- kudzera mu zokambirana

Sitidayambe kufalitsa Uthenga, koma kuonesetsa ngati anthu ali ndi chidwi ndi kuphunzira za Yesu.

Mwayi Kudzera mu Ntchito za Chikondi

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Banja Yolira

Banja lina losapemphera la ku Sgdaya,Benin, mwana wawo wa zaka 4 adamwalira. Kulira kwawo kunali kwakukulu kwambiri moti ngakhale mpesa wawo udali utacha, Iwo sadapite kukakolola koma amangolira. Mamembala a tchalitchi adapita kumunda kwawo kukakolola mbewu zawo zonse. Ndikuzibweretsa kunyumba kwawo. Banjali lidali lodabwa komanso lokhudzidwa. Adafunsa, 'Kodi mukuchitiranji izi?' Abusa adawawuza, 'Tidaona zimene zidakuchitikirani, ndipo tangofuna kukuwonetserani kuti ngakhale mudataya mwana wanu,chikondi cha Mulungu ndi chanube. Timakukondani, Mulungu amakukondani. Tangofuna kuwonetsa chikondi cha Mulungu kwa inu.'Iwo sadayitane banjali kuti ibwere ku tchalitchi,koma lamulungu lotsatiralo, banja lonse la anthu 12 lidabwera ku tchalitchi. Iwo adati, 'Ife tilipano chifukwa mudatithandiza, mudationetsera chikondi. Tabwera kuno chifukwa tikufuna kuti tikuthokozeninso, komanso tikufuna tipembedze Mulungu amene mukumutumikira'.

- Chidachitika ndi chani mu nkhaniyi?
- Kodi banja limafuniranji kuti ipembedze Mulungu? *(chifukwa tchalitchi cawaonetsera chikondi)*
- Kodi mukuganiza kuti banjali likadavomereza chimodzimodzi zikadakhala kuti abusa akadangowauza kuti akuyenera kulapa ndi kulandila Yesu? *(Ayi. Adali wokhumudwa kwambiri.)*

Ntchito za chikondi zimapangitsa anthu kuti afunse 'Mukuchitiranji zimenezi?' Titha kuwafotokozera kuti muli kuwathandiza chifukwa mukufuna kuti muonetsere chikondi cha Mulungu.

Ngakhale anthu amene tilikuwatumikira sadapereke moyo wawo kwa Yesu, timawaonetserabe chikondi. Iyi ndi njira yomvera Mulungu ndi kumulemekeza. Komabe, Mulungu amagwiritsa ntchito ntchito za chikondi kupangitsa anthu kuchita chidwi mwa Yesu. Ngati anthu akuoneka kuti akufunisitsa kumvabe zambiri, tikhoza kukhala wokonzeka kufalitsa uthenga.

Mwayi Kudzera Mokambirana

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Mulungu akhoza kupereka mwai kudzera mu zokambirana. Poyambilira,tidawerenga nkhani ya Yesu kuyankhulana ndi mkazi wa ku Samaliya. Tikawerengabe , tithakuona kuti Yesu akubweretsa Mulungu nkatikati mwa zoyankhula.

Zochita Mphunzitsi: *Funsani anthu awiri awerenge sewero yotsatirayi. (Palibe ntchito nimene ikufunika)*

Yesu ndi Mkazi wa ku Samaliya (Kuchokera ku Yohane 4:4-26)

Yesu: Ungandipatse madzi ndimwe?

Mkazi: Bwanji Inu muli Myuda, mupempha kwa ine kumwa, ndine mkazi Msamalia?

Yesu: Ukadadziwa mtulo wa Mulungu ndi Iye amene akunena ndi iwe, Undipatse ine ndimwe,ukadampempha Iye ndipo akadakupatsa madzi Amoyo.

Mkazi: Ambuye, mulibe chotungira madzi, ndi chitsime chili chakuya. Ndipo mwatenga kuti madzi amoyo? Kodi muli wamkulu ndi atate wathu Yakobo amene anatipatsa ife chitsimechi,namwamo iye yekha, ndi ana ake ndi zoweta zake.

Yesu: Yense wqakumwako madzi awa adzamvanso ludzu; koma iye wakumwa madzi amene Ine ndidzampatsa sadzamvanso ludzu nthawi zonse; koma madzi amene Ine ndidzampatsa adzakhala mwa iye kasupe wotumphukira kosatha.

Mkazi: Ambuye ndipatseni madzi amene kuti ndisamve ludzu, kapena ndisadze kuno kudzatunga!

- Kodi Yesu adayamba bwanji zokambirana? *(kupempha madzi)*
- Kodi Iye adangoyankhula za madzi, kapena adabweretsa Mulungu mu zokambiranazo? *(adayankhula za Mulungu)*
- Kodi Yesu adati akadamupatsa chiyani mzamayiyu chinthu chabwinokuposa chimene adamupempha? *(madzi a moyo,sadzamvanso ludzu)*
- Kodi mzimayiyu amawonetsa chidwi ndi zimene Yesu amanena? *(Eya)*

Mtumwi Paulo adapita ku gulu la anthu ku Atene kukafalitsa uthenga. Werengani Machitidwe 17:22-23.

- Kodi Paulo amanena chiyani mmene adanena za Mulungu? *(kupembedza mafano)*

Werengani Machitidwe 17:32-34.

- Kodi anthu adachilandira bwanji mmene Paulo amafalitsa uthenga? *(ena adali ndi chidwi, ena adalibe)*

Zochita Mphunzitsi: *Funsani anthu awiri awerenge sewero yotsatirayi. (Palibe ntchito nimene ikufunika)*
Ntchito yovuta

Simoni:	Iyi ndi ntchito yovuta! Kodi inu mukudziwa kuti pamene Mulungu adalenga dziko lapansi kudali kwapafupi kudzala chakudya? Kunalibe mafunde,kapena madzi osefukira kapena ng'amba. Adamu, munthu oyambilira kulengedwa ndi Mulungu, adaulima mundas koma sidali ntchito yovuta. Izi ndi zimene Baibulo likunena.
Marko:	Inde. Kodi ndi chifukwa chiyani tsopano ntchitoyi ikuvuta?
Simoni:	Ikuvuta chifukwa cha zinthu zonse zoipa zimene timachita ndi kuganiza. Baibulo imazitcha zinthu zoipazi tchimo.Mulungu adamuuza Adamu ndi Hava kuti asadye chipatso cha mtengo opatulika. Koma sanamvere Iye ndipo anadya chipatsocho. Kuyambila pamenepo, ulimi wakhala ntchito yovuta. Koma tsiku lina, Mulungu adzapanga chilichonse kukhala chatsopano.Sikudzakhalanso tchimo! Ndikadakuuza zambili ngati ungasangalare nazo.

- Kodi Simon amanena chiyani mmene amatchula za Mulungu? *(ntchito yovuta mmunda)*

Yesu, Paulo ndi Simoni onse adagwiritsa ntchito zokambirana za tsiku ndi tsiku kuti ayambe kunena za Mulungu.Adayesetsa kuwadabwitsa anthu za Mulungu. Aliyense akhoza kubweretsa Mulungu mu zokambirana, osati abusa okha, kapena atsogoleri a tchalitchi kapena alaliki. Ndiye, ngati anthu ali ndi chidwi kuti aphunzire zambiri,titha kufalitsa uthenga.

- Kodi ndi mavuto ati a tsiku ndi tsiku omwe anthu amawanena mdela lanu? (Fwa chitsanzo: Kodi anthu amachiona ngati cholemetsa kupereka nsembe kwa mizimu? Kodi anthu amayankhula za mavuto ndi ana awo kapena mabanja awo?)

Zochita Mphunzitsi:*Dikirani mpakana mitu yambiri ya maphunziro yaphunzitsidwa. Kenako mukhoza kufunsa:*

- Kodi mungabweretse bwanji Mulungu mukakhala kuti muli ndi zokambirana ngati izi?

NTCHITO YA GULU LALING'ONO
Awiri awiri, konzani sewero lalifupi. Wonetsani wina akubweretsamo Mulungu pamene akukambirana za umodzi mwa mitu imene takambirana.

KUPEREKA LIPOTI NDI CHIDULE
Funsani odzipereka achite sewero lawo kuyimilira gulu lonse. Funsani gulu lipereke zimene amva ndi mfundo zina.

Pamene mukunena za moyo mmene zimakhalira, bweretsanimo Mulungu. Funsani ngati anthu alisangalala nazo kuti atha kuphunzira zambiri. Ngati ali okondwa, mutha kufalitsa uthenga.

Kuchita nazo chidwi kapena ayi?

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
Mulungu akhoza kupereka mwayi kuti tifalitse uthenga kudzera mu ntchito za chifundo.Iye atha kupereka mwayi kudzera mu zokamirana zathu za tsiku ndi tsiku. Koma pamapezeka nthawi zina pamene anthu amaoneka kuti alibe chidwi chakumva mawu. Tiyeni tinene zokhudza zimenezi.

Werenganninso Machitidwe 17:32-34.

- Kodi Paulo adachitanji atayesa kuwakopa anthu kuti akhale ndi chidwi ndi kumva za Mulungu? *(adachokapo)*
- Kodi iye adapitilizabe kuwaumiliza anthu amene adalibe chidwi? *(Ayi)*
- Kodi adayankhula zambiri ndi anthu amene adali ndi chidwi? *(Eya)*

Ngati anthu alibe chidwi kuti amve zambiri, sitikuyenera kuwakakamiza. Mmalo mwake titha:

Pitilizani kupemphera.
Pitilizani kuchita ntchito zachifundo, ndikubweretsa Mulungu mu zokambirana.
Khalani okonzeka kugawana ndi aliyense amene ali ndi chidwi.

Ngati anthu akusangalatsidwa ndi kumva zambiri, titha kufalitsa uthenga. Mu phunziro lathu lotsatira tidzakambirana zoyenera kunena.

Mathero

Mulungu nthawi zina amagwiritsa ntchito machitidwe a chikondi kupereka mwayi kuti tifalitse uthenga. Iye akhoza kugwiritsa ntchito zokambirana zathu za tsiku ndi tsiku kuti atipatse mwayi umenewu. Tikufuna tiwaonetsere anthu chikondi cha Mulungu ndi kubweretsa Mulungu mu zokambirana zathu.

Ngati anthu avomereze ndi kuonetsa chidwi, titha kuwafunsa ngati nkotheka kuwauza za Yesu. Ngati anthu sakufuna atamva zina zambiri,titha kudikira. Tikhoiza pupitiliza kupemphera, kukonda ndi kubweretsa Mulungu mu zokambirana.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALING'ONO NDI PEMPHERO
Mmagulu a anthu awiri awiri kapena atatu atatu, ganizirani za wina amene mulinaye pa ubale koma samapemphera. Ganizirani za mutu kapena funso yomwe mungafunse kuti mumuthandize kuti ayambe kuganizira ndi kuyankhula za mzimu. Pempherani kuti Mulungu akuthandizeni kukwaniritsa dongosolo limeneli, ndipo Adzatsegula mtima wa munthuyo.

Phunziro 8: Kudzala Mbewu

Mfundo Yotsogolera
Zithunzi zinayi zitha kutikumbutsa kunena za Mulungu, Tchimo, Yesu, Nsembe ndi moyo wathu watsopano ndi chiyembekezo cha kumwamba.

Zipangizo
- Kadi ya ndondomeko ya ulaliki: kudzala mbewu.
- Makadi a maubale atatu:(makadi 4: Chilengedwe, Kugwa, Mtanda, Moyo wosatha)

CHIDZIWITSO CHAPADERA KWA MPHUNZITSI: *Phunziro ili likupereka Uthenga onse. Magulu ena azidziwa kwambiri mfundo zilimmenemu. Iwo aphunzira za uthengawu mwachangu. Ngati zokhudza Mulungu ndi tchimo sizikudziwika bwino ku chikhalidwe chanu, mukuyenera muphunzitsa pang'onopang'ono. Lolani nthawi ya mafunso. Ndizofunika kuti ophunzira aliyense amvesetse mbali iliyonse ya nkhani ya Uthenga. Mukuyenera kuzigawa mmaphunziro awiri.*

Chiyambi

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
Petro adatipula munda wake mosamala. Iye adachotsa miyala yonse ndi tchire ndi kugwira ntchito mu chonde chabwino. Adadikilira kwa masabata koma simudamere chilichonse mmunda mwake.

Zochita Mphunzitsi: *Nyamulani kadi ya ndondomeko ya ulaliki: kudzala mbewu*
- Kodi Petro adayiwala kuchita chiyani? *(kudzala mbewu)*

Ngati sudadzale, sungakolore. Kukhala mkhrisitu zili ngati choncho. Munthu sangayambe ubale ndi Mulungu ndi kukhala otsatira pokhapokhapo amve Uthenga wabwino.

Mu phunziro lathu lomaliza, Taphunzira kuti Mulungu atipatsa mwayi kuti tifalitse uthenga. Izi zitha kuchitika kudzera mu ntchito za chifundo kapena muzokambirana za tsiku ndi tsiku. Tikhoza kufalitsa Uthenga ngati anthu akuwonetsa kuti ali ndi chidwi chofuna kumva za Mulungu.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALING'ONO
- Kodi mudayesapo kufalitsa Uthenga?
- Ngati inde-, Chidachitika ndi Chiyani? Nenani chilichonse chabwino kapena choipa mudakumana nacho.
- Ngati AYI - Chifukwa chiyani? Chinavutitsa kuti Uthenga usafalitsidwe ndi chani?

KUPEREKA LIPOTI

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
Nthawi zina timafuna tifalitse Uthenga koma ndikovuta kudziwa kuti ngati tafotokozera bwino. Kapena sitidziwa kwenikweni kuti tinena chani.

Zochita Mphunzitsi: *Ikani makadi anai owonetsa maubale atatu pamalo pomwe ophunzira atha kuona mosavuta.*

Maphunziro oyambilira a TCT Amafotokoza za maubale atatu amene Yesu adawabwelera kuti awabwezeretse. Zithunzi izi zitikumbutsa choyenera kunena ndi anthu pamene tikudzala mbewu ya Uthenga.

Chilengedwe

Zochita Mphunzitsi: *Wonetsani* ***CHITHUNZI*** *1: Chilengedwe. Nkhaniyi ikuchokekera pa Genesisi 1-2. Mutha kuwerenga chidure cha nkhani mmunsimu kapena gwiritsani ntchito Baibulo.*

Anthu amafuna adziwe kuti Mulungu ndi ndani. Yambani ndi kuwauza nkhani yokhudza chilengedwe. Fotokozani zokhudza nkhani ndi tanthauzo lake pa ife.



NKHANI: Mlungu adalenga dziko ndi zonse zokhalamo. Chilichonse chimene adalenga chidali bwino. Mulungu adalenga munda wokongola kwambiri kuti anthu oyambilira , Adamu ndi Hava akhalemo. Pachiyambi, Mulungu ndi Adamu amayenda ndi kuyankhula wina ndi mzake mmunda wa Edeni. Adamu ndi Hava amakhala mwa mtendele wina ndi mzake. Dziko limene Mulungu adalenga limamupatsa Adamu ndi Hava zimene amafuna.

ZIKUTANTHAUZANJI KWA IFE: Mulungu sali ngati mizimu ina. Iye ali ndi mphamvu kwambiri ndi kulamulira pa chilichonse. Chilichonse mdziko ndi chake chifukwa adachilenga ndi Iye. Mulu7ngu ndi wabwino. Iye samachita cholakwika. Mulungu amafuna anthu kuti akhale pa ubale wabwino ndi Iye, wina ndi mzake ndi dziko.

Kugwa

Zochita Mphunzitsi: *Wonetsani* ***CHITHUNZI*** *2: Kugwa. Nkhaniyi ikuchokera mu Genesisi 3, Genesisi 12 ndi Eksodo*

Anthu amafuna kuti adziwe kuti tchimo ndi chiyani. Fotokozani nkhani ya kugwa,ndi kuti ikutanthauzanji kwa ife.



NKHANI: Mulungu adauza Adamu ndi Hava kuti asadye chipatso china chake mmunda wa Edeni. Adamu ndi Hava sadamvere Mulungu. Kusamvera Mulungu, kuchita zinthu zoipa, zimachedwa tchimo. Ichi chidapangitsa kuti choipa chilowe mdziko. Pamene Mulungu adabwera mmunda, Adamu adamubisalira Mulungu. Adamu ndi Hava tsopano amakanirana. Kuchokera pamenepo, anthu adayamba kumenyana wina ndi mzake. Malo adakhalano wovuta kulima. Anthu amayenera kugwira ntchito kuti akhale ndi moyo pa dziko. Zotsatira za tchimo ndi kuonongeka kwa maubale ndipo chimaliziro chake ndi chilango cha Imfa.

Mulungu amakhumba kubwezeretsa chimene chawonongeka chifukwa cha tchimo. Mulungu adapereka malamulo ake amene amaonetsa mafuno ake abwino ku mbali inailiyonse ya moyo.Koma palibe mmodzi amene akadatha kumvera malamulo onse molondola. Amapereka msembe kulipilira machimo awo., koma sizinali zokwanira.

ZIKUTANTHAUZANJI KWA IFE: Anthu onse ,ngakhale sitili kumudziwa Mulungu,timadziwa kuti zinthu zina zimene timachit a ndizolakwika. Tonse tidachimwa. Tchimo limapangitsa Maubale athu ndi Mulungu,wina ndi mzake, ndi chilengedwe kuti ziwonongeke.Nthawi zina timayesetsa kusinthanitsa zoipa ndi zabwino kapena zikhulupiliro za chipembedzo. Pena timakhumudwa, chifukwa sitingakhalenso anthu amene timayembekezera kuti tikhale.

Mtanda

Zochita Mphunzitsi: *Wonetsani* ***CHITHUNZI*** *3: Mtanda. Nkhani ikuchokera uthenga wa Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane.*

Anthu amafuna kudziwa kuti Yesu ndi ndani komanso atichitira chiyani. Fotokozani nkhani yokhudza Mtanda: Nenani za nkhaniyo, ndi kuti ikutanthauza chiyani kwa ife.

NKHANI: Mulungu adali ndi cholinga chofuna kubwezeretsa maubale amenene adawonongeka ndi tchimo. Kwa zaka 2,000 zadutsazo, Mulungu adatumiza mwana wake Yesu pa dziko. Yesu adabadwa ngati munthu. Iye adakhala moyo wosachimwa. Adalolera kuphedwa ngati nsembe yolungama yowombola machimo.Iye adafa pa Mtanda, kutenga machimo athu kwa Iye Yekha. Patatha masiku atatu, Iye adauka ndi kukhalanso ndi moyo,kuligonjetsa imfa. Iye ali mmoyo kufikira lero.



ZIKUTANTHAUZANJI KWA IFE: Yesu akhoza kukhululukira machimo athu. Iye akhoza kuchiza maubale athu ndi Mulungu, anzathu, ndi chilengedwe.Kuti tipulumutsidwe,timakhulupilira mwa Yesu. Timamupempha kuti atikhululukire machimo athu. Timapereka mbali iliyonse ya moyo wathu kuti tichite chifuniro chake. Ichi ndi chimene chimatanthauza kukhala Mkhrisitu.

Moyo Wosatha

Zochita Mphunzitsi*: Wonetsani* ***CHITHUNZI*** *4: Kubwerela. Yohane 3:16 ndi Chivumbulutso 21:1-7 ndi ndime zofunikira mu gawo limeneli. Ngati pali nthawi, lowezani Yohane 3:16 pamodzi.*

Fotokozerani zokhudza moyo wosatha:

Baibulo limati, Mulungu adakonda dziko lapansi kotero adapatsa mwana wake wokondeka kuti okhulupilira Iye asatayike koma akhale nawo moyo wosatha. Aliyense amene akhulupilire Yesu adzakhala kwa muyaya, ngakhale atamwalira.Moyo wa tsopano wayamba tsopano, pamene timaphunzira kumvera Mulungu.Ubale wathu uyamba kubwezeretsedwa monga mmene Mulungu amafunira kuti zikhale poyamba. Tsiku lina Yesu adzabweranso ndi kubwezeretsa zonse kwatunthu.'Sikudzakhalanso imfa kapena kulira kapena chisoni kapena zowawa'.Maubale onse atatu adzabwezeretsedwa kwa muyaya.



Kuyesa Kugawa Uthenga

Zochita Mphunzitsi: *Nyamulani kadi, mukamapanga ndamanga*

Uwu ndi uthenga umene tikufuna kugawa

Chithunzi 1: Chilengedwe: Mulungu adalenga dziko yolungama.

Chithunzi 2: Kugwal: Tchimo idalowa mdziko. Idawononga ubale wathu ndi Mulungu,wina ndi mzache ndi chilengedwe.

Chithunzi 3: Mtanda: Mulungu amatikonda kwambiri ndipo adatumiza mwana wake Yesu natifera kuti akabwezeretse ubale umene udawonongeka chifukwa cha kugwa. Tikhoza kufunsa Yesu kutichotsera machimo athu kuti ubale wathu uyambe kuchila.
Chithunzi 4: Moyo Wosatha: Titha kukhala kwa muyaya ndi ubale umene wabwezeretsedwa. Moyo wathu wa tsopano wayamba TSOPANO.

Kugawana uthenga ndi wina sizifunika kuchita kamodzi. Patha kukhala zokambirana zambiri kwa nthawi. Mukafalitsa, ndi ganizo labwino kufunsa,*'Muli ndi funso?'*. Izi zimapereka mpata kwa anthu kuti aganizire pa zimene amva. Akafunsa funso koma simukudziwa yankho lake, mutha kuwaitana ayankhule ndi Abusa anu.

Kachikena, MUSADANDAULE ndi kusowa kwa mawu abwino. Musadandaule kuti musiya chinachake osachinena. Ntchito yathu ndi yochita zimene tingathe, ndi kukhulupilira Mulungu kuti agwira ntchito mmitima ya anthu.

NTCHITO YA MZATHU
Zochita Mphunzitsi: *Gawani mmagulu a awiri awiri. Aliyense atenge mbali pogawa uthenga kwa mzake. Akuyenera kuganisira za zithunzi 4 zija. Pakatha mphindi khumi ndi zisanu, funsani magulu ena achitenso,panganinso komaliza. Ntchitoyi itha kutenga mphindi makumi anai ndi zisanu. Aliyense akhala ndi mwayi katatu kuti afotokoze za uthenga wabwino ndi mwayi katatu kutu amve zikufotokozedwa.*

KUPEREKA LIPOTI NDI CHIDULE
- Kodi kunali kusavuta kugawa uthenga koyamba kapena kachitatu?
- Ndi mafunso ati kapena mavuto ati amene mulinawobe?

Zochita Mphunzitsi: *Ngati wina ali ndi funso kapena vuto, funsani gulu kuti iyese kumuthandiza. Izi ziwaphunzitsa kudziwa kuyankha mafunso wokhudza uthenga. Zikuwonetseraninso, monga mphunzitsi,ngati pali pena pamene gulu lasokonezeka napo.*

Mathero

Sabata ino muli ndi ntchito!
- Yeserani kugawa uthenga kwa munthu mmodzi.(atha kukhala okhulupilira wina)

Pempherani kuti Mulungu apereke mwayi kuti mugawe uthenga ndi wina amene sadamudziwe Mulungu.

Phunziro 9: Kuyembekezera Mbewu Zatsopano

Mfundo Yotsogolera
Mulungu ali pa ntchito.Sitikuyenera kudera nkhawa pamene tikudikilira kuti anthu atsatire uthenga wabwino.Sitikuyenera kunenelera za chowona cha ubwino wa kutsatira Yesu.

Zipangizo
- Ndondomeko ya makadi a ulaliki.Kudzala mbewu ndi kudikilira mbewu zatsopano.
- Makadi a maubale atatu:(makadi anayi: Chilengedwe, Kugwa, Mtanda, Moyo wosatha).

Chiyambi

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKURU
***Zochita Mphunzitsi: N*yamulani** Kadi ya Ndondomeko ya Ulaliki: Kudzala Mbewu.
Mu phunziro lotsiliza, Tidanena za kudzala mbewu. Tidagwiritsa ntchito zithunzi za maubale atatu zomwe zimatithandiza kukumbukira choyenera kufotokozera. Tidayesera kugawa uthenga.

KUBWEREZA
Zochita Mphunzitsi: *Nyamulani makadi a maubale atatu, pamene mukufunsa mafunso otsatirawa. mayankho sakuyenera kukhala ofanana ndi amene alembedwa; kumbutsani gulu kuti sakufunikira mawu apadela,omveka bwino kuti afalitse uthenga.*
Chithunzi 1: Chilengedwe
- Kodi ndi chinthu chiti choyambirila kulalikira?
    - *Mulungu adalenga dziko labwinobwino.*
    - *Mulungu sali ngati mizimu ina. Iye ndi wamphamvu komanso ndiwabwino.*

Chithunzi 2. Kugwa
- Kodi chinthu chotsatira kulalikira ndi chiyani?
    - *Tchimo linalowa mdzikolo ndi kuphwanya ubale wathu ndi Mulungu, wina ndi mzake komanso chilengedwe.*

Chithunzi 3: Mtanda
- Kodi timanena chiyani zokhudza Mtanda?
    - *Yesu ndi mwana wa Mulungu.*
    - *Iye sanachimwepo.*
    - *Iye anafa pa mtanda ngati nsembe ya machimo athu.*
    - *Tikapereka moyo wathu kwa Yesu,Amakhululukira machimo athu ndi kumanganso ubale wathu.*

Chithunzi 4: Moyo Wosatha
- Kodi chinthu chomalizira kulalikira ndi chani?
    - *Titha kukhala kwa muyaya ndi ubale watsopano.*
    - *Moyo wathu watsopano wayamba tsopano.*

Zochita Mphunzitsi: *Nyamulani Kadi ya Ulaliki: Kudikilira Mbewu Zatsopano.*
Phunziro ili ndi yokhudza kudikilira mbewu zatsopano.

- Mukamaliza kudzala mbewu, mungathe kuona zimene zikuchitika pansi pa nthaka? *(Ayi)*
- Kodi mungaikakamize mbewu kuti imere? *(Ayi)*
- Kodi mlimi achitenji pamene akudikilira kuti mbewu zimere? *(Dikirani. Khulupilirani. Yembekezerani. Pemphererani zokolola zabwino.)*

Ulaliki uli ngati ichi. Mukamaliza kugawa uthenga anthu amafunikira nthawi. Sitikuyenera kunenelera kapena kugulitsa chilichonse. Timakhulupilira Mulungu kubweretsa anthu mu ufumu Wake.

Vuto ya Kulapa

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKURU

Munthu wa Chichepere wa ku Cambodia

Kunali Mtumiki wina ku Cambodia. Akhala akulalikira zokhudza Yesu ndi munthu wina wachichepere. Munthu ameneyi anakhumudwa atazindikira kutianali ochimwa ndipo amayenera kupita ku Gehena ngati chilango cha machimo ake.Koma pamene anaganiza zopereka moyo wakekuti akhale Mkhrisitu, sanafune kutero. Sabata Iliyonse amapita Mtumiki, ndikunena kuti, ndikufuna kukhala mkhrisitu. Mtumiki amayankha kuti, Kodi mukufuna mutasiya maloto anu ndi zokhumba zanu ndi kukhala wa Khrisitu Yekha? Kodi mukufuna mutasiya kupereka nsembe kwa milungu ya pamtundu,koma kupembedza Mulungu Yekha? Kodi mukufuna kukhala ndi nthawi yophunzira za Mulungu? Nthawi zonse mnyamatayi amapita atakhumudwa chifukwa samafuna. Koma, amachita mantha kudzalipira machimo ake ndikupita ku Gehena, concho amabwerabe sabata ndi sabata ndikufunsabe Mtumiki-Kodi pali njira ina yokhalira mkhrisitu? Mtumiki amayankha kuti, -Ayi,Ukuyenera kusiya moyomwako wa uchimo kupanda apo sungakhale mkhrisitu konse.

- Kodi chifukwa chiyani mnyamata anali wokhumudwa? *(Amafuna kuti akhululukidwe machimo ake pamene akuwachitabe)*
- Kokdi chifukwa chiyani Mtumikiyu sanapemphere naye kuti akhale mkhrisitu? *(Samafuna kumutsata Yesu)*
- Kodi mukuganiza kuti Mtumikiyu amalondola, osapemphera naye munthuyi kuti akhale mkhrisitu? Chifukwa chiyani? Kapena chifukwa chani kuti samayenera?

Kenako munthuyu anakumana ndi mtumiki wina ndi kumuuza kuti athedwa ndipo akufuna atakhala mkhrisitu. Mtumiki wachiwiriyu alali wokondwa – Munthu uyu akufuna atakhala mkhrisitu.Mtyumiki wachiwiriyu anamuuza munthuyu kuti chomwe akuyenera kuchita kuti akhale mkhrisitu ndi kunena pemphero la kulapa. Mnyamatayi anali wosangalala kwambiri – Panali njira ina. Chimene amayenera kuchita ndi kunena pemphero basi. Chinali chinthu chosavuta. Samamvetsetsa kuti ndi chifukwa chiyani Mtyumiki oyamba uja amazipanga kukhala zinthu zovuta kwambiri. Anapemphera pemphero ndi kubweleranso ku moyo wake wa uchimo, wosangalala chifukwa sakuyeneranso kudandaula kuti moyo wake upita ku Gehena. Panalibe mmodzi mwa Atumiki aja adaonanso mnyamatayi.

Nkhani tangowerengayi ikufanana kwambiri ndi nkhani ina imene ikupezeka mBaibulo.

Werengani Marko 10:17-22.

- Pamene Munthu wachuma atangofika, Kodi adafunsa chiyani? *(Ungalowe bwani moyo wosatha)*
- Kodi Yesu anamuuza chiyani munthu mnyamata wachumayi kuti achite? *(Agulitse zonse analinazo ndi*

kupereka kwa aumphawi)

- Kodi mnyamata wachumayi anayankha bwanji? Kodi adachita zimene Yesu adanena? *(Anapita wokhumudwa ndipo sadachite zimene anauzidwa)*
- Kodi munthu wachumayi anapulumutsidwa? *(Ayi)*
- Chifukwa chiyani sanapulumutsidwe? *(Samafuna kumumvera Yesu)*

Yesu amadziwa kuti munthuyu amakonda chuma chake osati Mulungu. Munthuyu samafuna kusiya chuma chake ndi kumutsata Yesu.Yesu sanalore kuti munthu wachumayi amutsate pokhapokhapo amvere Yesu mmadera onse a moyo wake.

- Ngati wina sakufuna kulapa ndi kumvera Yesu, Kodi kunena pemphero la kulapa ingamupulumutse? *(Ayi)*
- Kodi munthu wachichepere wa ku Cambodia uja anapulumutsidwa atanena pemphero la kulapa? *(Ayi, Iye sanasinthe)*

CHIDULE

Sitikuyenera kukakamiza wina kuti anene pemhpero la kulapa.Ndi Mulungu yekha amene angasinthe munthu ku afune kumutsatira Yesu. Tikuyenera kukhala wokhulupilika kukonza thaka ndi kudzala mbewu ya ulaliki. Tikhulupilire Mulungu kuti abweretse zokolola mu nthawi Yake.

Mulingo ndi Zofunikira

Tiyeni tiganize zifukwa zina zomwe zingapangitse kuti wina akhoza kukhala asakonzeka kutsata Yesu.

KUWUNIKIRA KWA MUNTHU PA YEKHA.

Zochita Mphunzitsi: *Werengani mafunso otsatirawa ngi kupereka mphindi ziwiri kuti munthu alingalire.*

- Kodi mukudziwa wina yemwe anabweretsa vuto m'banja lawo pamene adaganiza zomutsata Yesu? Mdera lawo?
- Zinali zosavuta kapena zovuta kwa inu kulingalira zomutsata Yesu? Ndi mtengo wanji womwe munayamba kuganizira? Ndi kusintha kuti kumene munachita mmoyo mwanu? Kodi zinali zoyenera?

KUWUNIKIRA KWA MUNTHU PA YEKHA

Zochita Mphunzitsi: *Itanani anthu kuti anene nkhani zaokhudza Zofunika pofuna kutsata Yesu.*

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Werengani Luka 14:25-33

- Potengera chigawo ichi, kodi chofunika kuti wna akhale Ophunzira wa Yesu ndi chiyani?
    - *Kudana ndi banja lawo poyerekeza ndi mmene amakondera Yesu.*
    - *Senza Mtanda - Kukhala ololera kupereka nsembe ndi kuzunzika chifukwa cha Yesu.*
    - *Kukhala ofuna kusiya chirichonse tilinacho.*
- Kodi chingakhale chiyani kuti osakhulupilira asasankhe kusintha kapena kulapa ndi kutsata Yesu? *(Mayankho atha kukhala awa: Kuvomereza kwa banja lawo, udindo, kapena ulemu wa mu dera, chitetezo, kapena kupembedza mizimu ina.)*

Werengani Mateyu 13:44-46.

- Kodi Mulungu amafanizira ufumu wa kumwamba ndi chiyani?
    - *Chuma*
    - *Ka nkhono*
- Kodi chuma chinali ndi kuthekera motani?
    - *Chilichonse anali nacho*
- Kodi anthu adali okhumudwa polipila dipo?
    - *Ayi, adali ndi chisangalalo*

Ngati wina anewna kuti akufuna kutsata Yesu, Akuyenera kuyesetsa kumvera Mulungu mu mbali iliyonse ya moyo wawo. Akuyenera kusankha Yesu pambali pa kulemekeza mabanja awo ndi amzawo. Ngati anthu saganizira mtengo uwu, sangathe kumvesetsa za kutsata Yesu Khrisitu.Koma Yesu ndi wodabwitsa kwambiri ndipo mtengowu ndiwoyenera!

NTCHITO YA MAGULU AANG'ONO

Zochita Mphunzitsi: *Sankhani mafuinso awiri amene akugwirizana ndi nkhani yanu.Perekani funso limodzi ku gulu limodzi ndi limodzi ku gulu lina. Pamene magulu akukambirana , akumbutseni kuti asanenelere kapena kukakamira.*

- Tangoganizani mwagawana uthenga ndi wina wake ndipo adanena kuti,'ndikufuna ndikhale ndi moyo wosatha, koma banja langa singandiloleze kuti ndikhale mkhrisitu.' Kodi mungachite chiyani kapena munganene bwanji?
- Tangoganizani mwagawana uthenga ndi wina wake ndipo adanena kuti,'ndikufuna kutsata Yesu'. Koma ndimapeza ndalama zanga kudzera mogulitsa mowa. Sindingathe kusiya zimenezi. Kodi mungachite chiyani kapena munganene bwanji?
- Tangoganizani mwagawana uthenga ndi wina wake ndipo adanena kuti, 'Ndikufuna kupembedza Yesu uku ndikupemphelerabe milungu ina ya kwathu.' Kodi mungachite chiyani kapena munganene bwanji?

KUWUNIKIRA KWA MUNTHU PA YEKHA

Ngati Wina Akana Ulaliki

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Ganiziraninso zokhudza nkhani ya munthu wachinyamata, wachuma ndi Yesu.

- Kodi wachinyamatayu anamulandila Yesu? (Ayi)
- Kodi Yesu anachita ntchito yoyipa pomulalikira munthu wachichepereyi? *(**dziwani:** funso ili likhoza kubweretsa kusokonezeka kwakukulu! Asiyeni akambirane kwa kanthawi ngati zikufunika kutero. Funsani mafunso monga,Kodi anthu ena amaganiza chiyani? Mukugwirizana nazo? Kodi chimampangitsa mlaliki kuti apambane ndi chiyani?)*
- Ngati tagawa uthenga, komabe anthu sanakhale akhrisitu, Tinalakwitsa? *(Ayi)*

Yesu sanachimwepo kapena kulephera. Iye amachita chifuniro cha Mulungu nthawi zonze molondola. Komabe atamaliza Yesu kunena ndi munthu wachumayi, sanapulumutsidwe. Ngati Mlaliki,titha kukhumudwa kuti ngati munthu sanapulumutsidwe,sitinachite bwino. Koma Mulungu ali okondwa nafe pamene tikumumvera Iye. Tihta kumukhulupilira Iye ndi zotsatira.

Kodi china ndi chiyani tingachite?

Choyenera chomwe tingachite ndiko kupitiliza kuwapemphelera kuti apulumutsidwe. Ndi Mulungu yekha yemwe amapatsa anthu moyo watsopano. Tikuyenera kupitiliza kuonetsa chikondi kwa munthuyo. Tikuyeneranso kupemphera,Mulungu, ndithandfizeni kuti ndidziwe chomwe ndingachite tsopano.Mulungu ationetsera zinthu zoyenera kuchita, mwa chitsanzo:

- Nenani umboni wanu
- Nenani ndime za mBaibulo ndi nkhani za mBaibulo.
- Uzani abusa kuti awayendere.
- Ayitaneni abwere ku tchalitchi kapena kuwerenga

Zitavuta bwanji, sitikuyenera kunenelera kapena kuwakakamira kuti amvetse. Yesu sadachite zimenezo ndi munthu wa chuma uja. Iye adasankha kumusiya apite, ngakhale chinali chopweteka.

Mathero

Pamene tikufalitsa ulaliki, Timafunikira kupanga mtengo wotsatira Yesu kukhala wosavuta. Sitikuyenera kuchita choncho. Mulungu adzathandizira anthu kuti amvetsetsekuti ndiodabwitsa bwanji ndi Kufunika kwake. Tikuyenera mokhulupilika, kuonetsa chikondi ndi kufalitsa uthenga. Tikhoza kukhulupilira Mulungu kuti agwire ntchito mmitima ya anthu.

Phunziro 10: Kuchokera ku Mmera Mpaka Chipatso

Mfundo Yotsogolera
Pamene anthu ali okonzeka, titha kuwaitana kuti atsate Yesu. Tikuyenera kuphunzitsa akhrisitu atsopano.

Zipangizo
- Ndondomeko ya makadi a ulaliki (makadi 6).

Chiyambi: Mbewu Zomera Kumene

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
- Ndi mafunso ati amene munafunsidwa pamene mumabatizidwa?

Zochita Mphunzitsi: Nyamulani Kadi ya ndondomreko ya ulaliki
Ngati wina afuna kukhala mkhrisitu, afunseni mafunso otsatirawa:
- Kodi ukukhulupilira kuti Yesu ndi yekhayo amene angakupulumutse ku tchimo lako?
- Mukufuna mutasiya kuchimwa ndi kuyamba kumvera Mulungu mmbali zonse za moyo wanu?

Zochita Mphunzitsi: *Uzani ophunzira kuti abwereze mafunso kambirimbiri**.***

Ngati wina anena Inde, ku mafunso amenewa, ali okonzeka kukhala mkhrisitu.Ili ndi Pemphero losavuta yomwe mungapemphere nawo. (Yuthanso kuwabweretsa kwa abusa anu kapena kwa mtsogoleri wina. Munthu ameneyo atha kupemphera nawo).

Yesu, Ndikupepesa chifukwa cha machimo anga. Ndikukhulupilira kuti ndinu Mulungu, ndipo Ndinu Wabwino. Chonde khululukirani machimo anga.Ndiyeretseni. Ndikupereka moyo wanga, moyo wanga wonse.

Mbewu Zomera Kumene Mpaka Chipatso

ZOKAMIRANA ZA GULU LALIKURU
Zochita Mphunzitsi: *Nyamulani Kadi ya Ndondomeko Yolalikira: Mbewu yatsopano ndi chipatso**.***
Pamene wina akhala mkhrisitu, Amakhala ngati mbewu yatso. Lero tikamba zokhudza kumene tingafike kuchokera pano *(nyamulani 'Mbawu ya tsopano')* kupita pano *(nyamulani 'Chipatso')*
- Kodi mukukumbukira cholinga cha Ulaliki? (*kubweretsa anthu mu Ubale ndi Mulungu kuti akhale Otsatira ake)*
- Timadziwa bwanji kuti wina ndi Otsatira wa Mulungu? *(amakhala ndi zipatso)*
- Kodi mbewu zatsopano zimaberekeratu zipatso nthawi yomweyo? (Ayi)
- Kodi ndi zinthu ziti zimene alimi amachita pamene mbewu zayamba kukula?
  (Mayankho olondola ndi monga: kuchotsa tchire, kuziteteza ku nyama, kuthilira ndi zina)

Zochita Mphunzitsi: *Nyamulani Kadi ya Ndondomeko Yolalikira: Kuthilira Mbewu Zatsopano*
Ulaliki sumaima ngati anthu akhala a Khrisitu. Monga ngati Mlimi, amasamalirabe mbewu zatsopano,tikuyenera kuthandiza okhulupilira atsopano kuti zikule.

Kuthilira Mbewu: Kuphunzitsa

ZOKAMBIRANA ZA MMAGULU ANG'ONO ANG'ONO
Werenganinso Ntchito yaikulu (Mateyu 28: 19-20).

- Kodi ndi mbali ziwiri ziti zopangira ophunzira? *(Kuwabatiza ndi kuwaphunzitsa asunge malamulo onse a Yesu)*
- Pamene munangokhala mkhrisitu, ndi zinthu ziti zomwe simumazi mvesetsa? Kodi ndi zinthu ziti zomwe ophunzira ambiri okhwima mu chikhrisitu amakuphunzitsani?
- Kodi ndi mbali ziti za moyo wanu wakale zimavuta kusintha kapena kuchoka?

KUPEREKA LIPOTI NDI CHIDULE

Ophunzira a tsopano sasinthiratu mwansanga ndi kukhala bwino. Ndi zachidziwikire kuvutikabe ndi uchimo. Maubale ena akhalabe ovuta. Sangachite ntchito zokomera Mulungu nthawi zonse. Tikuyenera kuwaphunzitsa kuti atsate Khrisitu mmbali zonse za moyo wawo. Chimenechi chimatchedwa Kutumikira chifukwa tikuthandiza wina kuti akhale ophunzira.

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
Vuto la Yoswa

Pamene Yoswa anakhala mkhrisitu, Anali wosangalala kwambiri. Machimo ake anakhululukidwa! Koma mmene masabata amapita,anayamba kumva kufooketsedwa. Kwa zaka zambiri, banja lake yakhala yovuta. Yoswa amaganiza kuti pamene anakhala mkhrisitu, banja lake likhala losavuta. Amaganiza kuti sadzakhumudwanso ndi mkazi wake. Yoswa amaopa kufotokozera anthu ena mu mpingo. Kodi anthu akadaganiza kuti Yoswa sanali Okhulupilira?

- Chifukwa chiyani Yoswa amva kufooketsedwa?
- Tingawathandize bwanji Okhulupilira atsopano kuti azinena mavuto omwe akukumana nawo? Ndi chani chimene chingakuthandizeni kumva kumasuka ,kufotokozera ena?

Ndi chinthu chabwino kuthandiza okhulupilira atsopano kuti adziwe kuti ndibwino kunena mavuto awo. Sangalandire thandizo ngati palibe wina amene akudziwa zosowa zawo. Titha kunena zotsamwitsa zathu kuchokera mmbuyo. Titha kunena mavuto amene tikukumana nawo tsopano. Ngati pali okhulupilira wina akuvutika, tikuyenera kuwonetsa kukhudzika ndi chikhululuko.

Njira Zabwino Zophunzitsira

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU
Werengani Aheberi 10:24-25

- Kodi ndime imeneyi ikunena kuti tizitani?
    - *Tilimbikitsane wina ndi mzake kukonda ndi ntchito zabwino*
    - *Osaleka kusonkhana kwathu pamodzi*
    - *Kulimbikitsana wina ndi mzake*

Ndime ikuti Osaleka kusonkhana kwathu pamodzi.Osasiya okhulupilira atsopano kuti akule mu chikhulupiliro chawo pawokha. Kumanani nawo pafupipafupi, osati kutchalichi kokha! Pa nthawi iyi mutha:

- KUWALIMBIKITSA:
    - Kuwapemphelera ndi kupemphera nawo.
    - Fotokozani chimene Mulungu achita ndi mmene akuchitira mmoyo wanu.
    - Itanani ena (anzanu,abusa anu) kuti abwere mudzagawane nawo.
    - Nenani nkhani ya mBaibulo kapena ndime za mBaibulo.
- KUWALIMBKIITSA kuti akhale okonda ndi ochita ntchito zabwino:
    - Kuwaitanira kuti apite ku maphunziro a Baibulo ndi inu.
    - Auzeni kuti atenge nawo mbali mmachitachita a chikondi pamodzi ndi Inu.

NTCHITO YA MZATHU

Zochita Mphunzitsi: *Gawani gulu kuti akhale awiri awiri. Perekani vuto limodzi limodzi kuchokera munsimu, womwe amadza pamene wina atembenuka mtima, pa uwiri wawo. (Sankhani vuto limene likugwirizana ndi okhulupilira atsopano mdera lanu). Auzeni akonze sewero lalifupi. Sewero likuyenera kuwonetsa wina akuphunzitsa okhulupilira watsopano pomulimbikitsa(pemphero,kugawana mawu)ndi kulimbikitsa.(Kumuyitanira ku maphunziro a Baibulo kapena AOL). Wnesetsani kuti anthu onse ali awiri-awiri achita sewero ndi kupereka mfundo.*

- Banja lawo lakwiya chifukwa akhala mkhrisitu.
- Banja lawo likufuna kuti azilambila milingu yawo.
- Mwana wawo wadwala, ndipo akukonzekera kupita naye kwa sing'anga.
- Amakhumba kumwa mowa akakhumudwa.
- Sagwirizana ndi mnansi wawo.

CHIDULE

Kuphunzitsa ophunzira kumatanthauza kuyenda mu moyo pamodzi. Timaonetsera okhulupilira osakhwima mu chikhulupiliro, angapemphere bwanji, kuwerenga Baibulo, ndi kukula mwa Khrisitu. Timawalimbikitsa kuti asasiye!

KUWUNIKIRA KWA MUNTHU PAYEKHA

Ganizirani munthun wina mu mpingo mwanu amene ndi okhulupilira, koma sakuoneka kukula ngati ophunzira. Mpemphelereni,ndi kufunsa Mulungu choyenera kuchita kuti mumuthandize kukula.

Kubwereza Buku la Ulaliki

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKULU

Tanena za Ulaliki kuti ulingati ulimi.Iyi ndi phunziro lomaliza mu maphunziro a ulaliki. Tiyeni tionenso mfundo zotitsogolera.

Zochita Mphunzitsi:*Ngati ophunzira sanapeze yankho, onaninso mfundo zotsogolera za mu phunziro pamodzi nawo kenako mufunsenso funsolo.*

Nyamulani Kadi ya kusamala nthaka

- Kodi cholinga cha ulaliki ndi chiyani?
    - *Kupanga ophunzira/ kukhala ndi ubale ndi Mulungu.*
- Kodi mlaliki ndi ndani? *Mkhrisitu Aliyense*

- Kodi Mulungu amagwiritsa ntchityo chiyani kuti asamale nthaka?
    - *Miyoyo yathu ya tsiku*
    - *Umboni wathu*
    - *Mapemphero athu*

Nyamulani Kadi ya kudzala mbewu

- Kodi chimene chingabweretse mwayi oti ukhoza kulalikira uthenga ndi chiyani?
    - *Machitachita a Chikondi*
    - *Mayankhulidwe a tsiku ndi tsiku*
- Tikamafalitsa uthenga, kodi ndi maubale atatu ati omwe amatikumbutsa kuti tigawane ndi anthu?
    - *Chilngedwe*
    - *Kugwa*
    - *Mtanda*
    - *Moyo Wosatha*

Nyamulani Kadi ya kudikilira mbewu

- Kodi tifunika kunenelera za kutsata Yesu? Ayi

Nyamulani Kadi ya mbewu zatsopano

- Kuni mukukumbukira mafunso awiri omwe tingafunse anthu amene akufuna kukhala mkhrisitu?
    - *Kodi mumakhulupilira kuti Yesu ndi yekhayo amene angakupulumutseni ku machimo anu?*
    - *Kodi mukufuna mutasiya kuchimwa ndi kuyayamba kumumvera Mulungu mu nyengo zionse za moyo wanu?*

Nyamulani Kadi ya kuthilira mbewu

- Pamene wina akhala mkhrisitu, Kodi tikuyenera kuchitabe chiyani?
    - *Kuwaphunzitsa/Kuwathandiza kuti akule mu chikhulupiliro.*

Nyamulani Kadi ya chipatso

- Kodi tingadziwe bwanji kuti wina ndi Ophunzira wa Yesu? *Amabala zipatso.*

Ngati wina awonetsa zipatso, timadziwa kuti ndi Ophunzira komanso ali ndi ubale ndi Mulungu.Ichi ndi chimene timati ndi ulaliki.

Mathero

ZOKAMBIRANA ZA GULU LALIKURU

- Kodi ndi chinthu chodabwitsa chiti chimene mwaphunzira mu punziro limeneli?
- Kodi ndichinthu chimodzi chiti chimene Mulungu akufuna inu kuti muyambe kuchita?
- Kodi mafunso ena ndi ati omwe mulinawo okhudza ulaliki?

Malangizo a Mphunzitsi: *Uzani ophunzira kuti ayankhe mafunso.Ngati pali mitu ina yoti munene,lembani munsimu kuti atsogoleri a TCT adziwe.*

Pemphelerani atengambali pamene akugwiritsa ntchito maphunziro amenewa.

Phunziro Lowonjezela: Kwa Azibusa

Mfundo Yotsogolera
Pali nkhani zambiri mBaibulo zimene zimathandizila okhuluilira kukula mchikhulupiliro chawo

Chiyambi

Nkhanizonse mBaibulo zimatiphunzitsa ife za Mulungu ndi kuthandiza okhulupilira kukula mchikhulupiliro chawo. Phunzilo ili likuphunzitsani inu mmene mungakonzere uthenga pogwiritsa ntchito nkhani za mBaibulo. Zimathandiziranso kuganizira mpaka nkhani makumi awiri za mBaibulo kuti mutha kuphunzitsa mosavuta. Nkhani iliyonse ya mBaibulo imawonetsa choonadi chofuynikira cha chimenea Mulungu ali ndi ubale wathu ndiiye.

Ngati ulibe kuthekera kokhala ndi Baibulo lako pezani abusa anzanu amene ali ndi kuthekela. Gwirani ntchito pamodzi kuti musinthe gawo linalirilonse kukhala nkhani ndi kuyi kumbukira. Choncho mutha kunena nkhani ku mpingo wanu.

Mungakonze Bwanji Uthenga Pogwiritsa Ntchito Nkhani za mBaibulo

Ndondomeko mmene mungapangire nkhani za mBaibulo

1. Mvetsetsani nkhani

   Werengani nkhani mBaibulo. Gani8zirani za nkhaniyo.

   i. Kodi nkhaniyo ikukuphunzitsani chiyani?
   ii. Kodi cholinga chenicheni ndi chani?
   iii. Mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani nkhaniyi inalembedwa mBaibulo?

2. Perekani chithunzithunzi cha nkhani

   Tangoganizani ngati munali mmodzi wotenga mbali mu nkhani. Dzitengeni nokha ngati mmodzi wa machitachita mu nkhaniyo. Kodi mungamve bwanji (mwa chitsanzo, ngati munali ofotokozera nkhani yokhudza alendo omwe anabwela kudzauza Abulahamu ndi Sara kuti pakatha chaka adzakhala ndi mwana.) Kodi Abulahamu akanamva bwnji ndi nkhani imeneyi Kodi Sara akanamva bwanji?

3. Kambani nkhani mokweza

   Mukhoza kufotokozera nkhaniyi kwa wina aliyense – Kwa mkazi wako, kwa mwana kapena kwa mzako. Kukamba nkhani mokweza zimathandiza kuganiza chofuna kunena. Mukangofotokozera nkhani mutha kulemba kapena ijambuleni kuti mukhoza kuikumbukira bwino.

4. Pitilizani kukambirana

   Kukambirana kumapangitsa nkhani kukhala yosangalatsa kwambiri. (Mwachitsanzo, ngati mukukamba nkhani yokhudza munda wa Ideni ndi njoka, onesetsani kuika mawu okhawo amene njoka yanena kwa Eva)

5. Fotokozani, ndi chifukwa chiyani nkhaniyo iliyofunika ndipo ikuphunzitsa chiyani za Mulungu ndi anthu.

   Pa nkhani zonse za mBaibulo zimene tapereka mu phunziro ili, zikupatsani Mfundo zina.

6. Perekani njira mmene tingazifanizire ndi miyoyo yathu

Anthu akuyenera kuchita zimene aphunzira,kapena sichikhoza kukhala mbali yawo ndi chikhalidwe chawo.
Yakobo 1:22-25 Akunena kuti, Khalani akuchita mawu osati akumva okha ndi kudzinyenga nokha.Chitani zimene mMawu akunena. Pakuti ngati munthu ali wakumva mawu osati wakucita, iyeyu afanafana ndi munthu wakuyang'anira khope yache ya chibadwidwe chache m';kalirole; pakuti wadziyang'anira yekha nachoka, naiwala pompaja nali wotani. Komai ye wakupenyerela m'lamulo langwiro ndilo laufulu, natelo chipenyere ameneyo posakhala wakumva wakuiwala komatu wakuchita ntchito adzakhala odala m'kuchita kwacha.

Nkhani Makumi Awiri za mBaibulo Zophunzitsa

Mu Buku yoyamba mwaphunzira nkhani yachirengedwe ndi kugwa. Mu buku la maphunziro a ulaliki, phunziro lachisanu ndi chitatu, mudafotokozera nkhani kuyambira Genesisi 1-2. Nkhani iyi imafotokoza kuti Mulungu analenga zonse. Ikutiphunzitsa kuti tchimo la munthu ndi imene inapangitsa kuti dZiko liwonongeke. Izi ndi nkhani zina zophunzitsa ndi Mfundo zina zofunika mungapezemo.

MALONJEZANO A MULUNGU KWA ABULAHAMU
Genesisi 12:1-9, Genesisi 15

- Mulungu anasankha Abulahamu chifukwa Abulahamu anakhulupilira Iye, osati chifukwa cha zimene Abulahamu adachita.
- Malonjezano a Mulungu sadalira pa Ife, Koma pa chikhalidwe chake chimenea sichisintha

ABULAHAMU NDI ISAKI
Genesisi 22:1-19

- Abulahamu adasankha kukhulupilira Mulungu ndi chinthu chimene amachikonda kwambiri
- Mulungu amapereka zinthu zones zimene Ife tizifuna

YOSEFE
Genesisi 37-45

- Mulungu amatha kugwiritsa ntchito nyengo zovuta ndi zowawa kuti akwaniritse cholinga chake.
- Mulungu amadziwa za mtsogolo ndipo zones zili mmanja mwake.

MOSE NDI ULENDO
Ekisodo 5-14

- Mulungu ndi wamphamvu kuposa milungu ina yonse. Akulamulira dziko lapansi.
- Mulungu adamva anthu ake
- Mulungu amasunga malojezano Ake.

MU CHIPULULU
Ekisodo 16, 17:1-7

- Mulungu adapereka zinthu zones zimene anthu ake amafuna. Ndi Mulungu zones ndi zokwanira.
- Mulungu amatsogolera anthu Ake.

KUPELEKEDWA KWA LAMULO
Ekisodo 20-21

- Mulungu amasamala mbali zones za moyo wathu

- Cholinga cha Mulungu pa ife ndi chabwino
- Anthu sanasunge Lamulo. Ife tonse timafuna mpulumutsi

NKHONDO YA KU YERIKO

Yoswa 6:1-21

- Mulungu amatimenyela nkhondo pamene timukhulupilira Iye
- Tikuyenera kumvera ngakhale sizikumveka bwino kwa ife.

DAVITE NDI GOLIATI

1 Samueli 17:1-50

- Mulungu atha kugwiritsa ntchito aliyense amene amukhulupilira.
- Ndi Mulungu tikhala ogonjetsa. Palibe chifukwa chochitira mantha.

YONA NDI CHINSOMBA

Yona 1-3

- Mulungu ali ndi chisoni pa anthu onse.
- Tikalapa machismo, Mulungu amatikhulupilira.

ELIYA NDI ANENERI A BALA

1 Mafumu 8:16-40

- Mukapembedza Mulungu, simuyeneranso kupembedza milungu ina.Munthu wina aliyeense akuyenela kusankha pakati pa kupembedza Mulungu kapena mafano.
- Mulungu wathu ndi Wamphamvu kwambiri kuposa mizimu ina ndi milungu ina yonse.

NG'ANJO WA MOTO

Daniele 3

- Mulungu akhoza kutithandiza mu nyengo zonse. Iye ndi wamphamvu kwambiri kuposa olamulira a dziko lapansi.
- Ngakhale Mulungu sanachite chimenea tikufuna, tiyenela kumukhulupilira ndi kumumvera.

NKHANI YA KUBADWA KWA YESU

Luka 1:26-38, Luka 2:1-21

- Yesu ndi munthu weniweni komanso ndi Mulungu weniweni. (Osati munthu wapadeladela, osatinso Mulungu anamuyerekeza ngati munthu).
- Yesu ndi Mesia wolonjezedwa, ndipo anabadwa kuti atipulumutse ife ku tchimo.

YESU ALETSA NAMONDWE

Luka 8:22-25

- Yesu ali ndi mphamvu pa zolengedwa.

YESU ACHIZA MUNTHU WOGWIDWA NDI ZIWANDA

Luka 8:26-39

- Yesu ali ndi mphamvu pa mizimu yonse.

YESU ANENA NTHANO ZIWIRI - NDALAMA YOTAYIKA NDI NKHOSA YOSOCHELA

Luka 15:1-10

- Munthu wina aliyense ndiwofunikira kwa Mulungu.
- Mulungu akufuna munthu wina aliyense alape machismo ndi kukhala mbali imodzi ya ufumu wake.

YESU ADZUTSA LAZARO KWA AKUFA

Yohane 11:1-43

- Yesu ali ndi mphamvu pa Imfa.
- Yesu amasamala za ife kwambiri ndipo amakhumudwa pamene ife takhum

PASAKA

Luka 22:14-20

- Yesu ndi Mulungu,koma anabwera kudzatumikira.
- Tikuyenera kutumikirana wina ndi mzakenso.

KUPACHIKIDWA NDI KUUKA

Luka 23:13-56, Mateyu 28:1-10

- Yesu anadzipeleka ndi kutifera ife. Anasenza machismo athu ndi kutitengela chilango cha imfa pa iye.
- Yesu ndiwamphamvu kuposa imfa; sitiyeneranso kuopa imfa.

TSIKU LA PENTEKOSITE

Machitidwe a Atumwi 2:1-12

- Pamene Yesu anakwela kumwamba, Anatumiza mzimu Oyera kuti Ukhalke mwa ife.
- Mzimu Oyera umatipatsa mphamvu kuti tikhale monga Mulungu amafunira.

KUSANDULIKA MTIMA KWA PAULO

Machitidwe aAtumwi 22:1-21

- Tapulumutsidwa mwa chisomo osati mwa ntchito zathu. (Paulo anali Mfalisi).
- Uthenga ndi wa wina aliyense.